


KUKHAZIKITSIDWA KWAUZIMU

 Zikomo inu, M'bale Neville. Mmawa wabwino, abwenzi. Wokondwa kwambiri kukhala pano mmawa uno, ndi kukhala ndi malonje awa kuchokera kwa abusa. Zimenezo zinali zabwino kwambiri. Oh, inu mukudziwa, kuyankhula za akavalo, inu mukudziwa, kuika zingwe pa iwo, iwo ankadziwa kuti ntchito inali ikubwera. Chabwino, izo, ndine wokondwa basi Ambuye amatipanga ife kukhala kavalo wogwira ntchito, kuti tizikhoza kugwira ntchito, apobe. Chotero, ife sitikhala konse, sitimatopa kwambiri nkomwe kuti tichite chinachake kwa Ambuye, ngati izo zitigwera ife kuti tichite izo. Ngakhale, pokhala wotopa kwambiri lero. Ine ndinangokhala ndi nthawi yoipa ya izo, mu masiku angapo apitawo.

² Ndikupita ku California, ndinachita kupita pa sitima. Ndipo, ine ndikukuuzani inu, kukamba za mabampu-mabampu! Njira yonse kunjira uko, maora fifite-firii kuti ndikafike kumeneko, ndipo ndinakafika kumeneko thuu koloko mmawa. Faivi koloko, ndinkayenera kudzuka ndi kupita kukalalikira msonkhano wapa walesi. Kenako, a Christian Business Men, ine ndinkayenera kulalikira kachiwiri ku msonkhano wawo wa maiko onse. Ndiyeno masana amenewo, ine ndinalalikira ku kachisi wina wamkulu wa Baptisti, ndipo kenako a . . . usiku umenewo. Ndipo kenako ndimangopitirira, kumayankhula maora angapo aliwonse, mpaka potsiriza tinathera Lolemba usiku ku Angelus Temple. Ndipo kenako ndinakwera sitima pa leveni, ndipo ndinakhala maora sikisite-foro pofika kunyumba. Chotero inu mukhoza kulingalira, kulowa, dzana, ndipo basi . . .

³ Ndipo, dzulo, mkazi wanga analandira mafoni fifite-chakuti osamvetseka, kuti ndibwere kudzapempherera anthu. Dzulo mmawa, wokha, mwaona, mafoni fifite-chakuti achilendo. Zoonadi, onsewo sanali akonkuno. Iwo anali—iwo anali mafoni a dziko lonse, koma basi, “Kodi, mungabwere ku Florida? Kodi mungabwere *kuno*? Kuno ndi ku Louisville.” Iwo . . . Iwe ungatege bwanji, mwa fifite-firii amenewo tsopano, kwa mmawa umodzi wokha? Chotero, inu mukhoza kulingalira.

⁴ Chotero, dzulo masana, ine ndinabwera kuti ndidzawone, pakati pa ena a abwenzi athu okonedwa, chimene nthenda ya mdierekezi ili. Mnyamata amene ine ndinkamudziwa zaka zapitazo, anali chithunzi kumene cha thanzi, mnyamata wooneka wa zamasewera. Ndipo tsopano ali pafupifupi usinkhu wanga, ndipo iye akhoza kudutsa nainte. Ndipo iye wagoni, akufa ku Henryville. Mzake wa m'bale wanga wabwino kuno, M'bale Neville, anali Kermit Spurgeon; abambo ake, mlaliki wa Uthenga, ndi mphunzitsi wa sukulu, ndipo mwamuna wamphamvu wabwino.

⁵ Ine ndinalowa mnyumba M'bale Neville atandiuza ine kuti mnyamatayo amafa, ndipo ife tinali ndi mwayi waukulu womutsogolera iye kwa Ambuye Yesu, dzulo, ku chipulumutso cha moyo wake. Ndipo mkazi wake ndi ine tagwirizana pamodzi ndipo tinamupempherera iye moonamtima, khansa itamudya iye; kuchokera pa mapaundi thuu handirede ndi chakuti, mpaka, ine ndikukayika kuti iye amalemera sikisite. Chotero, ife tikukhulupirira ndipo tikugwiritsitsabe, kuti Mulungu amuchiritsa iye. Kuti, ife sitikudziwa chimene chiti chidzachitike. Koma, chinthu chimodzi ife tikudziwa, kuti iye wadutsa kuchoka ku imfa wapita ku Moyo. Ndipo ine ndikulingalira zomwe abambo ake akhungu okalamba ankaganiza pamene uthenga umenewo unabwera kwa iwo, pambuyo pa zaka zonse zomupempherera iye, ndipo pambuyo pa zonse. "Muzimulera mwana mu njira imene iye akuyenera kuyendamo," mwaona. Ndipo ine ndikudziwa kuti iye anali ndi chitsanzo chabwino pamaso pake.

⁶ Kusuntha kuchokera kumeneko, kupita ku New Albany, kwa Akazi a Slaughter omwe ankakhala kunjira kuno, ndipo madokotala anali atamupatsa iye mpaka sikisi koloko, kuti akhale moyo. Chotero, izo zinali kwambiri, zomvetisa chisoni kwambiri, pomadikirira. Ndi malo osiyanasiyana.

⁷ Mnyamata wina ankakhala pafupi ndi ine kumeneko, iye ankangoyendayenda, mnyamata wabwinobwino, ankagwira ntchito ku Bell Telephone Company, pafupifupi usinkhu wa zaka twente-chakuti zakubadwa. Anali. . . Bambo wa ana atatu kapena anayi aang'ono. Mtsikana wake wamng'ono anagwa tsiku lina ndipo anathyola nkono wake. Iye anayamba kumwa dzanzi mdzanja lake; izo zinamupuwalitsa iye. Iwo sakudziwa nkomwe chomwe chiri cholakwika ndi iye. Iye wagona kunjira uko, ndipo apo iye ali.

⁸ Basi chinthu chimodzi pambuyo pa chimzake, ndipo matenda pambali iliyonse. Ndine wokondwa kwambiri kuti pali njira yotulukira. Ndine wokondwa kwambiri kuti ife sitikuyenera kukhala kuno kwamuyaya, ifenso, sichoncho inu? Ife tikanachita chiyani ngati ndikanakhala kuti ndizikhala m'nyumba ya tizilombo iyi kwanthawizonse? Ndine wokondwa kuti pali khomo lotseguka. Ndipo ndizo zonse zomwe dziko lapansi liri, ndi nyumba ya tizilombo basi. Ndizo. . . Mwamsanga basi pamene inu munganiza kuti tikuyenda bwino, ndiye apa pamabwera chinachake panjirayo, ndipo, komabe, apa pakubwera chinachakenso. Koma, ndine wokondwa kwambiri kuti pali njira yotulukira; wokondwa kwambiri kuti Ambuye Yesu wabwera ndipo watipangira ife njira, njira yopulumukirapo.

⁹ Chotero, mmawa uno, Mlango wanga Cox wokondedwa anali kundiuzwa ine kuti winawake anali kubwera, pamene timawapempha anthu akumeneko kuti abwere kuti

adzapemphereredwe, ndipo mwina sanathe kukhala koma maminiti pang'ono chabe. Ndipo kenako mwinamwake ine ndikanawapempherera iwo ine ndisanakhale ndi msonkhano, ndipo, ndiye, ngati iwo akanati abwerere.

¹⁰ Ndipo ine ndinaganiza, ndiye, kwa ena onse amene amafuna kutsalira, ine ndiwupanga uthenga wanga kukhala waufupi, mmawa uno, pokhala ndasasa mawu, ndi—ndipo ndiyenera kuti ndizipita nthawi yomwe ino ku msonkhano wina. Ndipo chotero ine...Ndipo msonkhano waku Chicago uyamba Loweruka likubwerali.

¹¹ Ndipo, kenako, ine ndikuganiza kuti ora lafika loti gawo ili la dziko likuyenera kulandira kuchezeredwa kwakukulu, pa kudza kwa m'bale wathu wolemekezeka, Billy Graham, ku Louisville, sabata ikubwerayi. Iye adzayamba nthawi yomweyo, Louisville, ine ndikayambira mu Chicago. Chotero, ine ndidzakhala nditabwerera, chonchobe, ine—ine ndikufuna kudzakumana naye iye, pandekha, pamene iye ali kuno. Ndipo abwenzi ena adzandiwonetsa ine kwa iye. Ndipo ine ndakhala ndiri mu mzinda womwewo, kutsidya kwa nyanja, ndi malo ambiri osiyanasiyana, koma basi, chotero, ife sitinakwanitse kukumana wina ndi mzake.

¹² Ndipo ine—ine moonamtima ndikupempha mpingo uno, ndi gulu lino la anthu limene lasonkhana pano mmawa uno, kuti atenge msonkhano uwu pa mtima wawo, uko mu Louisville.

¹³ Ine ndikufuna kunena ichi, basi mwa njirayo. Kodi inu mukudziwa kuti eyite-seveni peresenti ya zakumwa zoledzeretsa zimachokera ku Louisville, Kentucky, ndizo—zimene zimamwedwa mu United States? Eyite-seveni. Kodi inu mukudziwa, pafupifupi nainte peresenti ya fodya yense ndi zinthu zimachokera ku Louisville, Kentucky? Kodi inu mumadziwa kuti umenewo ndi mpando wa Satana. Iwo ndithudi uli. Iwo ndithudi uli.

¹⁴ Amodzi mwa malo olimba kwambiri amene alipo mdziko, ndi dera lino lozungulira kuno, kuti liswedwe chifukwa cha Ambuye Yesu Khristu. Ndi angati anapita kumeneko akulira misonzi, akuyesetsa kuti aliswe dziko lino, Mizinda ya Mathithi iyi, kwa Ambuye Yesu! Penyani, Erickson, onsewo amene ankatulukako, ngakhale akuchita kulira, za momwe iwo anayesetsa ndi kuyesetsa ndi kuyesetsa. John Sproul anachita kusweka, ku Glory Barn uko, akuyesetsa mwakuthekera kwake kuti achiswe chinthucho chifukwa cha Ambuye Yesu. Momwe ena ayimira pa nsanja, kudutsa Mizinda ya Mathithi iyi, ndi kuyesetsa, ndipo sanathe kuiswera iyo kwa Ambuye Yesu.

¹⁵ Tsopano, ine ndikuganiza Billy Graham ndi mmodzi wa amuna odziwika bwino amene alipo mu dziko lero, mu chipembedzo, mwa kulingalira kwanga. Zooni, tiri ndi mabishopu ndi maakibishopu. Koma, mwa kulingalira kwanga,

iyе ndi mlaliki wa Uthenga, munthu wa Mulungu. Ndipo chotero—ndipo chotero ine ndikuganiza kuti iye...Monga ankhondo Achikhristu, pamodzi, tiyeni tidziyike tokha ndi mitima pamodzi, ndi kupempherera msonkhano umenewo, kuposa kale. Ndi kupempha kuti Mulungu, mwanjira ina kapena imzake, atipatse ife miyoyo, ndi kuswa mpando wa Satana, kuti iwo atseke malo ofulula mowa aliwonse ndi kuwotcha mafakitale a fodya, ndi kudzazitsa mipingo ndi kukhala ndi kutsanulira kwenikweni kwa kachitidwe-kachikale ka Mzimu Woyera. Ambuye adalitse!

¹⁶ Tsopano, ine ndiri ndi chinachake chosiyana pang’ono, chosazolowereka pang’ono choyambira. M’bale wanga ali ndi mwana pano amene iwo akufuna kuti aperekedwe kwa Ambuye. Ndipo ine ndikuganiza ife tichita izo basi tisanapempherere odwala, ngati Mulungu alola. Ndipo ngati Mlongo Gertie angabwere pa limba. Ndi onse amene ali ndi ana aang’ono. . .

¹⁷ Tsopano, mu Baibulo, ife timaphunzitsidwa apa kuti... Tsopano, ambiri—ambiri, anthu ambiri, amati kuwabatiza iwo, kuwakonkha madzi ena pa iwo, amawutcha iwo “wamakanda” ubatizowo. Chabwino, tsopano, izo ziri bwino. Inde. Musamuvulaze mwanayo, ndipo ine—ndikutsimikiza kuti zikhala bwino. Ndipo, ena, ali ndi njira zina zomwe amachitira izo. Ndipo, koma, ife nthawizonse timakonda, mwapafupi basi momwe ife tingathere, kukhala ndi njira ya Baibulo yochitira izo. Ndipo, njira ya Baibulo yochitira izo, palibe malo mu Baibulo pamene iwo anayamba achitapo izo, ndi makanda. Anali. . .

Chabwino, tsopano, pamene Chipangano Chakale, iwo ankawapanga mdulidwe.

¹⁸ Ine ndikudabwa ngati akuluakulu angapo angamusunthire mlongoyo pang’ono pokha ku mbali imodzi apa, ngati mungatero, mpaka titakhala ndi kumpereka mwana; mlongo amene ali pa machira apa. Ndipo, chotero, inu simukusamala, mlongo wokondedwa? Ndi mphindi chabe. Ndipo ife. . .

¹⁹ Ndipo chotero ndiye, mu Chipangano Chakale, iwo—iwo ankamuchita mdulidwe mwana. Ndipo mu. . .Iwo ankamuchita mdulidwe mwana.

²⁰ Ndipo mu Chipangano Chatsopano, njira yokhayo imene iwo ankachitira izo, iwo ankawabweretsa ana kwa Ambuye Yesu, ndipo Iye ankawanyamula iwo mmanja Mwake, ndipo ankawadalitsa iwo. Ndipo anati, “Lolani ana adze kwa Ine, ndipo musawaletse iwo, pakuti Ufumu uli kwa otere.”

²¹ Tsopano ngati pali mayi wina aliyense pano, amene ali ndi mwana wawo wamng’ono, amene akufuna amupereke kwa Ambuye, ife tikhala okondwa kuchita izo nthawi ino. Ndipo tsopano mulole ife. . .mwatcheru.

²² Tsopano, dzina la mwana wamng'onoyu ndi ndani? [M'baleyo akuti, "Robert Lynn."—Mkonzi]. Mnyamata wamng'ono, Robert Lynn. Tsopano, izo nzabwino mwamphamvu. Tsopano, izi ziri. . . ndikukhulupirira inu—inu munamutenga kuti muzimulera mwanayo. . . ? . . .

²³ Izi zikuwonetsera a—mtima wa mayi kwa mwana. Ndipo poganiza za izi, iwo posakhala ndi ana aliwonse, komabe ankafuna kulera mmodzi, iwo anamutenga wamng'ono uyu kuti amulere. Kodi inu mukuzindikira kuti tonsefe ndife ana otengedwa kuti tileredwe? Mulungu anatikonda ife kwambiri, mwakuti anaitenga ife mwa Mwana Wake, Khristu Yesu. Ndipo ife tonse ndife ana otengedwa kuti atilere. Ndipo, kumbukirani, pamene abambo ndi amayi awa akuganizira za wamng'ono uyu amene analibe nyumba yoti apiteko, iwo anamupatsa iye nyumba, kuti amulere iye ndi kumusamalira iye. Ife tinalibe nyumba yoti tipiteko, ndipo Mulungu anatipatsa ife imodzi.

²⁴ Ndi mwana wotengedwa kuti aleredwe. Dzina lake ndi Robert Lynn Branham; mwana wokongola kwambiri, wamng'ono.

Tsopano tiweramitse mitu yathu.

²⁵ Atate athu ofunika Akumwamba, monga mmasiku apitawo, momwe abambo ndi amayi ochuluka anakwezera ana awo aang'ono m'manja Mwanu! Ndipo Inu munati, "Lolani aang'ono adze kwa Ine, ndipo musawaletse iwo, pakuti Ufumu wa Kumwamba uli wa oterewa." Ndipo wamng'ono uyu wopanda nyumba, wapatsidwa nyumba, ndipo Inu mwayika mmitima mwawo chikondi kwa mwana uyu.

²⁶ Ndipo, Atate, ife tikupemphera kuti Inu muwadalitse amayi ndi abambo awa, pamene iwo akumulera mwanayu. Ndipo mulole iye aleredwe mu nyumba ya pemphero, ndi kuti aziphunzitsidwa kupita ku tchalitchi, ndi kukhalira moyo Ambuye Yesu. Mdalitseni iye, Atate okonedwa Akumwamba.

²⁷ Ndipo, tsopano, ngati Inu mukanakhala pano pa dziko lapansi, mu thupi lanyama momwe ife taimira mmawa uno, iwo akanampereka mwanayu mu nkono Wanu. Koma Inu munapita Kumwamba ndipo munatidzoza ife kuti tipitirize utumiki mpaka Inu mudzabwere. Ndipo, Atate, pamene m'bale wanga wamagazi yemwe akumuyika mwanayu mmanja mwanga, ine ndikumpereka iye kwa Inu mu Dzina la Khristu. Mdalitseni mwana uyu ndipo mulole iye akhale wamoyo ndi kukhala wathanzi ndi wamphamvu, ndipo akule kudzakhala wantchito Wanu. Adalitseni abambo ndi amayi, mnyumba. Ife tikumpereka iye kwa Inu, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Amen.

²⁸ Akudalitse iwe, Agnes, ukhale mayi weniweni; ndipo iwe, Jesse, bambo weniweni kwa mwana uyu. Ndipo Mulungu akudalitseni inu mu kuyesetsa kwanu. Ndipo Mulungu akhale nanu inu.

29 Muli bwanji! Dzina la mwanayu ndi ndani? [Mlongo akuti, “Robert Darrel.”—Mkonzi]. Robert wina. Chabwino, izo ziri bwino. Robert Darrel.

30 Ndipo dzina lanu ndani? [Mlongo akuti, “Robertson.”—Mkonzi]. Ndiwe wamng’ono. [“Inde.”] Ndi dzina lanu lotsiriza? [“McCloud.”] McCloud. [Malo opanda kanthu pa tepi.]

Kubweretsa mitolo, kubweretsa mitolo,
Oh, tidzabwera mokondwera, kubweretsa
mitolo.

Kufesa mmawa, kufesa nthawi ya usiku,
Kufesa masana ndi usiku wa mame;
Pofika nthawi yokolola, kenako nthawi
yokunkha,
Tidzabwera tikukondwerera, kubweretsa
mitolo.

31 Chabwino, izo ziri bwino. Kubweretsa mitolo, ndicho chimene abambo ndi amayi amachita: kuwabweretsa iwo kwa Ambuye Yesu.

32 Mlongo wagona pa machira, akuwoneka woyipitsitsa kuposa onse, momwe ife tikuwonera. Iye ali pa machira. Ndipo ife tikanati... Ngati pali winawake... Iye akufuna kuti adikirire maminiti pang’ono chabe, kuti amve Uthenga, asanapemphereredwe. Ndipo ine ndikuganiza kuti ndi zabwino, kwambiri kwabasi. Ngati pali winawake pano amene sangathe kudikira, ndipo akufuna kuti achoke, ndipo ngati inu mukufuna kuti mupemphereredwe tsopano, ife tikhala okondwa kuchita izo, ngati inu mungakweze mmwamba dzanja lanu. Ngati sichoncho, ife tikhala ndi msonkhano wa machiritso mwamsanga ukangotha... uthenga waufupi; kungoyesera kuti zigwirizane ndi kalasi ya Sande sukulu. Chabwino. Kenako ife tiwerenga Lemba ndi kudzakhala ndi Uthenga ndipo, mwamsanga, ndipo kenako titenga nthawi yathu mu mzere wa pemphero.

33 Ndipo tsopano, ife tisanayambe, ine ndikufuna inu, nonse amene muli bwino mmawa uno, kuti muziwakumbukira iwo amene akudwala, chifukwa tikuyenera kupemphererana wina ndi mzake.

34 Ndipo ine ndinali wokondwa kwambiri pamene ine ndinafika ku California tsiku lina, ndi kulowa mu makachisi awo amene iwo ankayesera kukankhira panja. Ndipo ku Clifton iwo anali atayima kuposa mdadada wa mzinda, kunjja uko pa msewu, akungofuna kuchitira umboni. Ndipo akuti, “M’bale Branham, ine nthawi ina ndinali ndi khansa. Inu munandipempherera ine. Ine—ine ndinali wakhungu. Ine ndinali *ichi*.”

35 Ndipo kumatsika ndi msewu, ndi kumverera koteroko! Ine ndinaganiza, “Mulungu, zidzakhala bwanji tikadzawoloka ndi kubwera kutsidya linalo? Ndi awo apo, atasonkhana mmateni

sauzande, ataima pamenepo.” Ndipo chidzakhala chinthu chodabwitsa bwanji pa nthawi imeneyo! Chomwecho, ndiye, khama lathu lotopa laling’ono silidzatanthauza mochuluka kwambiri. Tsopano ife timapita mpaka ife basi, zimawoneka ngati, ife sitingapitirire patsogolo pena, ndipo basi timangotopa ndi kungokankhirapo.

³⁶ Ndipo kenako Satana amabwera, ndikudzati, “Ndi za ntchito yanji zimenezo? Iwe ukuchitira chiyani zimenezo?” Mai!

³⁷ Komano iwe ukaganiza za zinthu monga zimenezo, izo zimasintha izo, pamodzi. Izo zimapangitsa. . .Izo zimapangitsa zinthu kukhala zosiyana.

³⁸ Tsopano, ife tisanayandikire Mawu, ife tingapemphere kachiwiri mphindi yokha.

³⁹ Atate athu Akumwamba, ndi mitima yoyamikira kuti ife tikubwera kwa Inu. Ndithudi, Ambuye, Inu mmadziwa kopangidwe kalikonse ka munthu. Ndipo momwe iye aliri wofooka ndi wosalimba, ndi momwe iye ali wopanda mphamvu. Ndipo chowiringula choterocho ngati a—wantchito Wanu, munthu ali, koma, Ambuye, Inu mwa chisomo Chanu mwatiyitana ife kuti tikhale wantchito Wanu. Ndipo ife tikuzindikira, mmawa uno, za kusayenera kwathu, ndipo ife tikupempha kuti Inu mutilandire ife, Atate, lero, ndipo mutidzoze ndi Mzimu Woyera, ndipo muyankhule kwa ife Mawu achitonhozo amene Inu mwawayankhula mu Mawu Anu Oyera apa. Ndipo ife tikupemphera kuti Mzimu Woyera utengere Mawu aliwonse mpaka ku mtima, basi kumene iwo akuyenera kukakhalako, ndipo kumeneko iwo akazikike ndi kukula kukhala chisangalalo chachikulu, mitengo ya chipulumutso. Perekani izi, Atate.

⁴⁰ Achiritseni odwala ndi osowa. Ife tikudziwa kuti iwo ali pano. Ndipo ambiri abwera kuchokera mamailosi ambiri, ndipo agona mmahotelo ndi zinthu, kuyembekezera mwayi woti apemphereredwe. Ndife okondwa kwambiri chifukwa cha mwayi waukulu uwu, Ambuye, kudziwa kuti Inu muli pano kuti muchiritse odwala.

⁴¹ Mulungu, amodzi a odwala kwambiri amene ife tikuwadziwa, ndi mwamuna ndi mkazi wodwala tchimo. Ine ndikupemphera, Atate Akumwamba, kuti tsiku lino, kuti Inu mutero, mwanjira yapadera, mudzoze, lero, ndi kupulumutsa otayika. Mwamuna ndi mkazi aliyense wotayika, mulole iwo abwere mokoma ku Mpandowachifumu wa chisomo ndi kudzapulumutsidwa, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Khristu. Amen.

⁴² Tsopano Ambuye awonjezere madalitso Ake ku kuwerenga kwa Mawu Ake, pamene ife tikulowa mwa Iwo. Ine nthawizonse ndakhala wokhulupirira wamkulu mu Mawu. Pakuti, kuno, ndi mausiku angapo apitawo, ine ndimayankhula kwinakwake pa—

aneneri amene anapita kukanenera. Koma, Mikaya . . . aneneri foro handirede atapereka khoma limodzi lolimba. Komabe, Yehosafati anati, “Kodi palibe mmodzi winanso?” Mmodzi winanso, foro handirede anali atatha kupereka Mawu? Koma, Mikaya anakhala ndi Mawu a Mulungu. Iye anadziwa kuti panali chinachake cholakwika.

⁴³ Ndipo bola ngati timva chirichonse kunjwa kwa Mawu a Mulungu, ife timadziwa kuti pali chinachake cholakwika. Izo sizimamveka bwino bwino. Yesu anati, “Nkhosa Zanga zimadziwa Liwu Langa, ndipo mlendo izo sizidzamutsatira.”

⁴⁴ Ndipo zikomo inu, chifukwa chopemphera kunjwa uko, chifukwa cha chitsitsimutso chaku Angelus Temple. Usiku woyambirira kumeneko . . . Iyo imangotenga fifite-faivi handirede; faivi sauzande, faivi handirede. Iwo analowetsamo sikisi sauzande, ndipo ozimitsa moto anadzatseka zitseko, pa ola limodzi ndi theka ndisanafike kumeneko, ku Angelus Temple. Ndipo momwe Ambuye wathu Yesu wokonedwa anapulumutsira otayika ndi kuchiritisa odwala! Izo zinali zopambana. Ndipo tsiku lotsatira . . .

⁴⁵ Ndipo Mlongo wathu wamng’ono Hicks, amene anali mphunzitsi wa Sande sukulu kuno, ine ndinakomana naye iye ndi ana ake ndi mwamuna wake. Ndipo ine ndinakumana ndi M’bale Ben Bryant ndi onse amene anapita kuchokera ku kachisi yu, kunjwa uko, cha kumadzulo, ku—kukayanjana kunjwa uko. Kunali kukumananso kopambana bwanji, kudzawonana nawonso iwo kachiwiri!

⁴⁶ Mu mutu wa 17 wa Mateyu Woyera, basi mwanjira yowerenga, mmawa uno. Ine ndikufuna kuti ndiwerenge gawo chabe apa kwa mutu. Ndipo mulole Ambuye atipatse ife nkhani mu Mawu.

. . . patapita masiku sikisi Yesu anamtenga Petro, Yakobo, ndi Yohane m’bale wake, ndipo anawatengera iwo mmwamba pa phiri lalitali,

Ndipo anasandulika pamaso pawo: ndi nkhope yake inawala ngati dzuwa, ndi zovala zake zoyera monga kuwala.

Ndipo, taonani, pamenepo anawonekera kwa iye Mose ndi Eliya akuyankhulana ndi Iye.

Kenako Petro anayankha, ndipo anati kwa Yesu, Ambuye, kuli kwabwino kuti ife tikhale kuno: tidza . . . tiyeni timange . . . ngati inu mungafune, tiloleni ife tikupangireni inu akachisi atatu; mmodzi wanu, . . . winayo wa Mose, ndi wina wa Eliya.

Pamane iye anali chiyankhulire, onani, mtambo wowala unawaphimba iwo: ndipo taonani liwu linatuluka kuchokera mu mtambo, limene linati, Uyu

ndi Mwana wanga wokondedwa, mwa yemwe Ine ndikondwera; mvereni inu iye.

47 Ambuye awonjezere madalitso Ake ku kuwerenga kwa Mawu Ake.

48 Nthawizina Mulungu amakumana mu uphungu wosiyanasiyana wa munthu. Mulungu nthawizonse amakonda kuchita uphungu ndi munthu. Ndipo nthawi zambiri, mu Chipangano Chakale, momwe ife tingabwerere mmbuyo kuti tikapeze momwe Mulungu anakumanirana ndi munthu. Ndipo mosalabadira za kuchuluka kwawo, Mulungu amakumana ndi munthu. Iye anakumana nawo nthawi ina ndi faivi handirede. Ndipo Iye anakumana, kachiwiri, ndi sevente. Iye anakumana, kenanso, ndi thwelofu. Iye anakumana kamodzi ndi atatu. Ndipo kenako Iye anakumana, kachiwiri, ndi mmodzi yekha. Ndipo mosalabadira kuchuluka kwa uphungu, Mulungu nthawizonse amakonda kukumana ndi munthu.

49 Chotero, ngakhale mpingo mmawa uno usakhale waukulu mwa osonkhana kapena mu usinkhu, monga ma kafiduro ambiri aakulu lero, koma Mulungu adzakondwera kukumana nafe. Pakuti, Iye anati, “Paliponse pamene awiri kapena atatu asonkhana mu Dzina Langa, Ine ndidzakhala pakati pawo. Awiri kapena atatu akadzasonkhana mu Dzina Langa, Ine ndidzakhala pakati pa awiri kapena atatu amenewo.”

50 Ndipo chithunzi chimene ife tingayike pano lero, mwa Mzimu Woyera, ife tikhoza kutenga maora kuti tikumbe kulowa mu mutu umenewo, inde, ine ndingati kwa masabata. Ndipo Iwo wakhala ukukumbidwa, kwa zaka, ndipo, komabe, theka silinavumbulutsidwebe kuchokera ku mutu wopambana uwu, ndipo mwina sitidzatero konse.

51 Chifukwa, Mawu a Mulungu sali ngati mawu a munthu. Mawu a munthu amakhala ndi tanthauzo lina, kapena kufotokoza ndi nthawi imene anaperekedwa, koma Mawu a Mulungu amakhala ndi tanthauzo Lamuyaya kudutsa mmibadwo pamene Iwo akuyendererabe. Kam’badwo kalikonse kakhoza kutenga Mawu omwewo, chifukwa Iwo ndi odzozedwa, Amuyaya, osatha, kulengeza kosazilala kochokera kwa Mulungu. Ziribe kanthu ngati Iwo...Ngati atumwi ankawerenga Iwo mu m’badwo wawo, Iwo ankatanthauza chinachake kwa iwo; ngati Wesley ankawawerenga Iwo mu m’badwo wake, ndi Luther mu m’badwo wake, ndi Calvin mu m’badwo wake. Komabe, lero, Iwo akadali apobe anzeru komanso owala, ndipo akadali ndi mphamvu zochuluka basi monga Iwo anachitira ndi iwo pa tsiku limene Iwo anayankhulidwa, chifukwa Iwo ndi Mawu a Mulungu.

52 Mawu athu, kungoti, “Yohane, bwera kunyumba kwanga, ndikhala wokondwa kukuwona iwe.” Amenewo ndi mawu athu, ndipo amangotanthauza, “Yohane, bwera kunyumba kwathu.”

53 Koma pamene Mulungu ayankhula, izo ndi Zamuyaya. Iwo anapumidwa kuchokera ku mpweya weniweni wa chisavundi, Mlengi wosatha Iyemwini. Chotero, choncho, palibe njira yopezera tanthauzo lathunthu la kufotokoza kulikonse kwa Mulungu. Iwo ndi a m'badwo uliwonse, ndi kam'badwo kalikonse.

54 Tsopano, mu nkhani iyi, mu...chimene ife tiri nacho patsogolo pathu mmawa uno, anali Mulungu akuyankhula kwa anthu atatu.

55 Tsopano, *firii*, choyamba, ndi nambala yosankhidwa ndi Mulungu ya “ungwiro.” Mulungu anasankha firii, ndipo firii ndi nambala ya Mulungu ya ungwiro. *Seveni* ndi nambala Yake ya “kupembedza.” *Fifite* ndi nambala Yake ya “chisangalalo.” *Forte* ndi nambala Yake ya “yesero.” Ndipo firii ndi nambala Yake imene Iye anasankha yopitira mmwamba, lero.

56 Tsopano, firii ndi nambala ya ungwiro, ndiko kuti, kuti Mulungu amapangidwa wangwiro; Mulungu mmodzi, woona, Wamuyaya amapangidwa wangwiro mu timbadwo titatu ta mawonetseredwe a Umulungu Wake: Atate, Mwana, Mzimu Woyera. Sizitanthauza kuti pali amulungu atatu osiyanasiyana. Koma, alipo Mulungu mmodzi woyimiridwa mwa atatu. Mulungu si atatu. Mulungu ndi mmodzi. Koma, mawonetseredwe atatu a Umulungu Wake, kutanthauza, timbadwo titatu ta nthawi padziko lapansi timalungamitsa Mulungu mmodzi, woona ndi wamoyo.

57 Iye anawonekera kwa Abrahamu mu chitsamba chonyeka moto, ndipo anawatsogolera ana a Israeli, mu Dzina la Mulungu, Atate, kumene kunali Kuwala kumene kunapachikika pa kachisi, kumene kunawatsogolera iwo mu ulendo wawo. Mulungu, Atate. Ndipo kenako Atate, ndi cholinga chakuti adzabweretse chiyanjanitso pakati pa Mulungu ndi munthu . . .

58 Monga ine ndimayankhula kuno nthawi ina mmbuyomo, ine ndikukhulupirira, nthawi yotsiriza imene ine ndinali ku kachisi, pa nkhunda ndi mwanawankhosa. Momwe kuti Mulungu, yekha, . . . Panalibe wina akanakhoza kuchita zimenezo. Mulungu an kayenera adzabwere pa dziko lapansi ndi kudzaichita ntchitoyo Iyemwini. Ndipo pamene Iye anamuimira Mwana Wake mmawonekedwe a Mwanawankhosa, wofatsa mwa zolengedwa zonse, ndipo Iye anadziyimira Yekha mmawonekedwe a nkunda, yofatsitsitsa mwa mbalame zonse zowuluka mmwamba. Ndipo chifukwa chimene Iye anachitira izi, ndikuti adzatisonyeze ife kuti kufatsa kokha kudzakhala ndi kufatsa, kudzichepetsa kudzakhala ndi kudzichepetsa. Izo zikuyenera kugwirizana.

59 Kalipentali, kapena wopanga kabati, amene amadziwa chimene kulumikizana kumatanthauza, ife timadzitcha izo, kupanga miponje, kapena kulumikiza matabwa. Kupanga

bolodi likhale lokwanira, ndikumikiza matabwa. Ndipo iwo akabwera pamodzi, iwo amalumikizana molimba pamodzi. Atakhala ndi madzi pa iwo, iwo angafufume mpaka ngakhale mpweya sungathe kudutsapo.

⁶⁰ Ndipo pamene wokhulupirira ndi Mulungu... Mulungu amakhala wangwiro kwambiri, mwakuti, kupyolera mu kudula ndi kuwumbidwa kwa wokhulupirira, pamene iwo abwera pamodzi. Petro anati, “Lapani, kenako, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu, ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.” Mukuona? Zimawapangitsa iwo kukhala athunthu kwambiri!

⁶¹ Kenako pamene Mulungu anadzatsika mu mawonekedwe a nkunda, ndi kudzatela pa Mwanawankhosa ndipo nkudzakhala mwa Mwanawankhosa, ndipo sanamusiye konse Mwanawankhosa, pakuti iwo anali mmodzi. Icho chinali chimodzi mwa zochitika zazikulu kwambiri chimene dziko linakhalapo nacho. Tiyeni tingoyang’ana pa izo kwa mphindi chabe, kuchokera pa mutu wanga, koma momwe miyamba ndi dziko lapansi zinakumbatirirana. Momwe Mulungu ndi munthu anayanjanitsidwa pamodzi! Mmene kuti ngakhale zolengedwa zimene zinkawuluka mmiyamba, ndi zirombo zimene zinkayendayenda muthengo, zinadzakhala chimodzi, pamene munthu ndi Mulungu anayanjanitsidwa pamodzi, ndi Mwamuna, Ambuye Yesu Khristu. Ndi chinthu chopambana bwanji!

⁶² Kuti mukhale ndi Mulungu, khalani odekha. Mulungu ndi wodekha. Kuti mukhale ndi Mulungu, khalani ndi chikondi. Mulungu ndi chikondi. Khalani ofatsa. Khalani... Musamakhale odzidalira nokha. Nthawi zonse muzidalira pa Iye. Musamagwiritse ntchito malingaliro anuanu; muzitenga maganizo Ake. Muzilola maganizo Ake azikhala maganizo anu. Ndipo muziwatengera Iwo mmalingaliro anu achithupithupi, ndi kuwabwerezanso Iwo. Ndipo muziti, “O Mulungu, chotsani kukaikira kwanga konse, ndipo mulole maganizo anga akhale maganizo Anu.” Ndipo anthu odwala inu, muzichita zimenezo pamene ife tikuyankhula. Mungochotsapo, nkutayira kutali lingaliro la matenda. Mutenge malingaliro amachiritso a Mulungu, mulole Iwo akhale lingaliro lanu.

⁶³ “Taganizirani pa zinthu izi,” Baibulo linati, “ngati pali chiyamiko chirichonse, ngati kuli ukoma uliwonse.”

⁶⁴ Atatuwo, Mulungu akuyankhula ndi iwo. Tsopano, zitatu ndi chitsimikizo. Iye anatenga limodzi ndi Iye, Petro, chikhulupiriro; Yakobo, chiyembekezo; Yohane, chikondi. “Chikhulupiriro, chiyembekezo, ndi chikondi, zitatu izi.” Ngati inu mungakhale ndi chikhulupiriro ndi chiyembekezo ndi chikondi, inu muli pafupi ndi Ufumu wa Kumwamba, pamenepo; zinthu zitatu zazikulu. Mulungu anatenga zimenezo ngati chitsimikiziro,

chifukwa, “Pakamwa pa mboni ziwiri kapena zitatu, mulole mawu onse akhazikitsidwe.”

⁶⁵ Kenako, kachiwiri, izo zinaimira kukhazikitsidwa kwa mwana. Mu Chipangano Chakale, mwana akabadwa mu banja, ankapatsidwa mphunzitsi kuti amulere iye ndi kumusamalira iye. Bamboyo amakhala munthu wotanganidwa kwambiri, pa ufumu wake. Ndipo ufumu wawung’ono uliwonse unatchedwa nyumba.

⁶⁶ Umo ndi momwe, mu kumasulira kwa King James, Yohane 14, anati, “Mu nyumba ya Atate anga muli nyumba zazikulu zambiri.” Tsopano, izo sizimamveka bwino kwenikweni kwa anthu akumadzulo amene amatenga nyumba yayikulu ndi nyumba kukhala zosiyana. Koma mmasiku a kulembedwa kwa Baibulo, nyumba yayikulu imakhala mnyumba, pakuti nyumba inkatanthauza ufumu.

⁶⁷ Ndipo bambo uyu amakhala ndi antchito ambiri pa famu yake, paliponse, ambiri a iwo. Ndipo pamene mwana abadwa, iye amakhala ndi munthu wosankhidwa, wophunzitsidwa, wodzichepetsa, munthu wosankhidwa amene amakhala mmodzi wa chifuwa chake, gawo la ufumu wake, mphunzitsi. Wa mtundu wokhawo amakhala amene bamboyo ankamuyika woyang’anira mwana wake.

⁶⁸ Ndipo momwe Atate lero ayikira Mphunzitsi wamtundu woyenera pa ana Ake, inu ndi ine. Wosankhidwa, osati wina aliyense koma mtima weniweni ndi moyo wa Ambuye Yesu, kuti akalere mu chiyamikiro cha Mulungu.

⁶⁹ Momwe mphunzitsi uyu amayenera kusankhidwa! Iye amayenera kukhala munthu wanzeru, munthu wosankhidwa, wokonda abambo, amene azidzaphunzitsa mwanayo mfundo zolondola zokhazokha.

⁷⁰ Ndipo momwe Mzimu Woyera, lero, pamene Iye wabwera, zinthu zina zonse zikuwoneka kuti zimakhala zotsatira kwambiri pamene Mzimu Woyera wabwera. Anthu akhoza kunena kuti, “Masiku a zozizwitsa anapita,” koma mungomolola munthu yemwe ali wobadwa mwatsopano mwa Mzimu Woyera, kamodzi, abwere pamaso pa zimenezo. Pakuti, Iye amangophunzitsa icho chimene chiri chenicheni. Iye amangoyankhula za Atate.

⁷¹ Ine kulibwino ndikhale ndi munthu amene samadziwa ma ABC ake, kuti azimphunzitsa mwana wanga, amene anali ndi Mzimu Woyera, kuposa mapurofesa onse mdziko amene analibe Mzimu Woyera. Pakuti, Iye amayankhula za Atate. Mukuona? Ndipo Mzimu Woyera umayankhula za Atate. Ndipo kenako Iwo udzamuphunzitsa mwanayo, “Kuti asamakankhidwire uku ndi uku ndi mphepo iliyonse ya chiphunzitsa,” koma kuvomereza ndi kukhulupirira mfundo zimene Atate anaziyala.

⁷² Ndi chifukwa chake machiritso Auzimu amakhala ophweka kwambiri, kwa wokhulupirira weniweni, chifukwa iye waphunzitsidwa, ndi Mzimu Woyera, kuti azikhulupirira zinthu zonse. Kodi ife tingakayikire bwanji Mawu a Mlengi?

⁷³ Kodi dziko linakhalapo chotani? Kodi Mulungu anazitenga kuti zipangizo zoti alipangire ilo? Kodi inu munayamba mwayima kuti muganizire za zimenezo? Iye anangoyankhula izo. Ndipo, kuwonjezera apo, chirengedwe kumene chimene chiri pano tsopano si chinanso kuposa Mawu a Mulungu akuwonetseredwa. Taganizani za zimenezo. Mitengo imene imamera, ndi Mawu a Mulungu. Mapiri amene amafika mu mlengalenga, ndi kutipangitsa ife, ngati tikufuna kuti tiwone kukongola, tiyang'ane mmwamba pa phiri. Ndipo pamene mukukwera phirilo, ndi pamene ilo limakhala lowala ndi loyera.

⁷⁴ Nditayima kutsidya mminda ya madzi owundana ya kumpoto kwa British Columbia! Pamene mukuyang'ana apa, pa dambo; pokwera pang'ono, madzi amayenda oyera, amasanduka abuluu ndi oyera, mitengo imazimirira. Chirengedwe chonse chimakhala ngati chikuti, "Yang'anani mmwamba." Ndipo pamwamba pa chipale chowundana chachikulu icho chowala kwambiri mpaka chimawala ngati dzuwa, iwe ukamayang'ana mmwamba. Ngati iwe ukufuna kuwona zinthu zamphumphu ndi zenizeni, ndi zinthu zoyera, nthawizonse uziyang'ana mmwamba. Phiri limaloza izo. Davide anati, "Ndidzayang'ana kumapiri kumene kumachokera thandizo langa. Thandizo langa limachokera kwa Ambuye."

⁷⁵ Mphunzitsiyo nthawizonse ankamulozera mwanayo kwa abambo, ndi kuti amayenera kukhulupirira abambowo. Ndipo, kenako, mphunzitsiyo amakhala wophunzitsa.

⁷⁶ Mmawa uno, pamene ine ndimayang'ana pa mzanga wokonededwa wamng'ono, ndipo ine ndinawona mwana wanga wamng'ono, pamene iye anaponyera mkwiyo wake waung'ono pa tebulo, ndi mbale yake yaying'ono ndi mazira ake ndi zinthu, amayi anali atagwira ntchito mokhulupirika kuti amukonzere kadzutsa wake. Ndipo iwo anali kuyesera kuti amuphunzitse iye kudya ndi supuni yake. Ndipo iye amafuna atenge dzanja lolakwika.

⁷⁷ Chabwino, kwa ine, ine ndinati, "Musiyeni iye akhale ndi dzanja limenero." Koma amayiwo amadziwa kusiyana kwake. Iwo amadziwa, ngati amusiya iye kumapitirira mwanjira imeneyo, iye adzakhala wogwiritsa ntchito manja onse kapena adzakhala wamanzere, ndipo izo sizabwinobwino. Chotero, monga mphunzitsi weniweni, anamupangitsa iye kuti asinthe dzanja, ngakhale iye sanazikonde izo. Koma, amayiwo amadziwa chimene chinali chopambana.

⁷⁸ Ndipo nthawi zambiri, mphunzitsi wathu, Mzimu Woyera; ife timayesera kuchita izo molakwitsa. Koma, nthawizina

izo zimatipweteka ife. Nthawizina ife tikhoza kugona pabedi la mazunzo. Nthawizina adokotala akhoza kunena kuti ziyembekezo zonse zapita. Koma, ndi Mzimu Woyera ukutiphunzitsa ife kuti tigwiritse ntchito dzanja lamanja. Iye amadziwa zomwe ziri zabwino. Iye amadziwa momwe Atate amafunira kuti izo zizichitikira. Iye ndi mphunzitsi. Ndipo ine ndinaganiza . . .

⁷⁹ Joseph wamng’ono, iye samafuna kugwiritsa ntchito dzanja, chotero amayi anafikira mmwamba ndipo anatenga ndodo yake yofewa, yotalika pafupifupi choncho, ndipo iye anamugogoda iye pambali. Iye anayang’ana kwa ine. Koma, komabe, ine ndimamukonda iye ndi mtima wanga wonse, ndikanamufera iye momasuka, koma ine ndinkadziwa kuti amayi amadziwa bwino kwambiri. Ine ndinati, “Iwo akumuphunzitsa mwanayo.”

⁸⁰ Ife sitingafune kumveredwa chisoni, ndi kumveredwa chisoni, mochulukwa kwambiri. Ife tiyenera kumamvetsera kuphunzitsa mwana kwa Atate athu. Iye amadziwa zomwe ziri zoyenera. Nthawizina ife timati, pamene Uthenga ukulalikidwa, “Oh, ine ndingopita ku tchalitchi changa, iwo samatero . . . Eya, ine ndingokhulupirira Izo mwanjira *iyi*.” Mukuona? Koma, kumbukirani, Mzimu Woyera umadziwa bwino. Iwo umadziwa momwe ungakuphunzitsire iwe. Nthawizina umamenya ndodo, umakukonza iwe. [M’bale Branham anagogoda pa guwa—Mkonzi]. Inu mukuyenera kukumbukira, Mulungu anamupanga Iye kukhala a—wophunzitsa mwana wa Mpingo. Ndipo Iye amawakonda Atate, ndipo Iye nthawizonse amalozera kwa Atate.

⁸¹ Ndipo, tsopano, pamene mwanayo ankaphunzitsidwa, izo sizinkatanthauza kuti mwanayo . . . Mwanayo ndithudi ndi mwana wa abambowo. Koma ngati iye anali mwana wosamvera, mphunzitsiyo nthawizonse azikhala ndi vuto ndi iye. Nthawizonse, amakhala ali mkati ndi kunja, mmwamba ndi pansu. Chabwino, ndiye, uthenga uwu unkayenera kubweretsedwa kwa bambo, pamene bamboyo wawufuna. “Kodi mwana wanga akuchita bwanji?”

⁸² Kenako ankayenera kunena kuti, “Iye sakuchita bwino kwambiri.” Chabwino, ndiye, ndithudi, izo zinkakhumudwitsa mtima wa bamboyo.

⁸³ Ndipo izo zikutero lero, pamene Mzimu Woyera ukuyenera kuti ubweretse umboni wathu pamaso pa Mulungu. Pamene ife tikhala ana a Mulungu, timayenera tiziyenda moyenerana ndi ntchitoyo. Ife tiyenera kumayenda moyenerana ndi chirichonse chimene Mulungu wayika kuti ife tichite. Pakuti Mzimu Woyera ukutiphunzitsa ife, kuphunzitsa mwana. Kodi munayambapo . . .

⁸⁴ Pamene ndinali mnyamata, abambo anga anali osiyana ndi momwe abambo ena amakono aliri lero. Bambo

anga ankakhulupirira mu kupereka zikwapu, ndipo iye ankaziperekadi izo. Ife timazikumbukira izo. Ndipo ine, komabe, lero, wa zaka forte-seveni, ine ndikuzikumbukira izo. Koma izo zinandichitira ine ubwino. Zinandiphunzitsa ine. Ngati ndingapite kupita kumanda lero ndi kukamudzutsa iye, chinthu choyamba chimene ine ndingakachite ndi kugwira chanza manja ake ndi kumukumbatira iye pa zimene anachita.

⁸⁵ Ngati ine ndikumverera mwanjira imeneyo za abambo anga a padziko lapansi, kodi zidzakhala bwanji tsiku limenero pamene ife tidzayima mu Kukhalapo Kwake? Pamene, ife tidzawona zinthu zikuchitika kwa ife kwa ubwino wathu, kuti Iye amachita kutidula ife pang'ono pokha apa, ndi kutipanga ife kuphunzitsa-mwana, ndi kuchotsapo zinthu za mdziko, ndi kutilola ife tiziyenda monga ana odzichepetsa pamaso pa Iye. Zikhoza kuwoneka zovuta pachiyambi, koma Mulungu amadziwa zimene Iye akuchita. Ndithudi. Iye amadziwa zimene Iye akuchita.

⁸⁶ Ndipo Iye, ndiye, pamene Mzimu Woyera uyamba kubweretsa Mawu, ndiye, ngati mwanayo wakhala wosamvera pamene afika wokhwima, usinkhu wokhwima, ndiyeno, mwanayo nthawizonse amakhala mwana wamwamuna, ndithudi, koma iye amataya chinachake.

⁸⁷ Ndipo apa pali mfundo imene ndikufuna kuyifikitsa kwawo. Mulole Mzimu Woyera utengere iyo ku mtima uliwonse wa inu okhulupirira. Basi chifukwa chakuti ndinu wokhulupirira, ndithudi inu muli nawo Moyo wosatha; Mulungu ananena chomwecho. Koma kodi inu mungafune kungolowa mkati, monga Yobu ananenera, “Ndi khungu la mano anu”? Kodi inu mungangofuna kubwera pamaso pa Atate, ndi luso limene Iye wapereka kwa aliyense wa inu, monga kukhala wosamala, inu basi simunagwiritse ntchito ilo, kapena munalola chinachake chidzaima mnjira yanu? Inu munalola zinthu zazing'ono zomwe sizitanthauza kanthu kwa inu, kuwonjezera apo, kukangana pang'ono, ndi kudyana, ndi kutsutsana, ndi zotsemphana za mpingo, zimachotsa kufatsa ndi ubwino mmoyo wanu. Kodi inu mungafune kudzaima pamaso pa Atate monga choncho? Sindikukhulupirira kuti inu mungatero. Ine sindikukhulupirira kuti mungatero. Inenso sindingatero.

⁸⁸ Momwe ine ndimafuna kuti Iye adzanene, “Unachita bwino izo.” Osati ndi khungu la mano anga; koma, “Unachita bwino izo, mtumiki Wanga wabwino ndi wokhulupirika. Lowa mu zikondwerero za Ambuye, pakuti unachita bwino ndi zimene ukuyenera kuchita.”

⁸⁹ Mwina ndinu mayi wapakhomo. Ngati inu muli, Mulungu anakupangani inu kukhala mphunzitsi wa ana anu. Chitani ntchito yabwino ya izo. Mosalabadira zimene inu mukuyenera kuchita, muzichite izo bwino.

⁹⁰ Zindikirani, ndiye, ngati mwanayo anatsimikizira kuti anali woyeneradi zinthu zimene abambo anali nazo mu ufumu wawo, ndipo anakhala ali mwana wokhulupirika kwenikweni, ndiye mphunzitsi ankatumiza uthenga kwa abambo ake, “Oh, mwana wanu. . .”

⁹¹ Oh, tsopano, umenewo ndi Uthenga umene ine ndikufuna kuti Iye abweretse wa inu ndi ine. “Oh, mwana Wanu, malingaliro ake onse ali pa Inu. Zonse zimene iye akuyesera kuchita ndi kukondweretsa Inu. Iye amakhala ndi chidwi kwambiri mu zochitika Zanu, mpaka ndikovuta kuti mungamuletse iye.”

⁹² Kulibwino ndingokhala wachangu pang’ono pa Ufumu wa Atate kuposa kukhala wopanda changu nkomwe, pa Iwo. Kulibwino ndigwire ntchito mopitirira muyeso. Ndipo monga mlaliki wa Mpingo wa Khristu anandiuzira ine, nthawi ina kale, “Bambo Branham, kulibwino—kulibwino nditope kuposa kupanga dzimbiri.” Ndipo izo ndi zonga mochuluka. Kulibwino nditope, “ndi kufa mu zingwe,” zonga M’bale Neville ananenera, kuposa kukana kuvala zingwe. Sungalephere kuchita chirichonse moyipa kuposa kunyalanyaza kuyesera. Tiyeni tichite zonse zimene tingathe ndi zomwe mukuyenera kuchita nazo. Ndipo Mzimu Woyera, Mphunzitsi wathu, azibweretsa izo kwa Atate.

⁹³ Ndipo tsopano, zindikirani, ngati mwanayo akhala mwana wochirimika, ndiye izo zinkanenedwa kwa abambo ake. Ndipo pa. . . Oh, ine ndimangowakonda Mawu! Pa nthawi yoyikika, yoyikidwa ndi abambo okha, mwanayo amakhala. . . ulemelero ndi ulemu wake zimawonekera pamaso pa anthu. Bamboyo amamutenga mwana wake yemwe, amamukonzera chikondwerera, ndipo ankamutengera iye kwa kumalo opezeka anthu. Pambuyo pake. . . Pokhala mwana wake yemwe, wobadwira m’nyumba yake yomwe, komabe, mwanayo ankaikidwa pamalo m’banjamo, kuti alandire zinthu zonse zimene abambo anali nazo. Inu mukuziona izo?

⁹⁴ Tsopano, ngati ife tikhale akhalidwe labwino, tsiku lina laulemelero ife tidzakhala olandira zinthu zonse. Mulungu, mu tsiku Lake loikika, limene Iye adzaweruze anthu onse mwa Khristu Yesu. Nthawi ikudza imene Mulungu adzapereke mphoto kwa iwo amene anali okhulupirika, ndi kukanidwa kwa iwo amene alephera kukhala okhulupirika.

⁹⁵ Basi kupita kwa Ambuye Yesu kusanachitike. . . Mulungu pokhala mwa Iye; Nkhunda ikutsogolera Mwanawankhosa. “Iye sanabwere kuti adzachite za Zake yekha, koma kuti adzachite chifuniro cha Atate amene anamutuma Iye.” Iye anatsogozedwa ndi Mzimu, kuti akamutenge Petro, Yakobo ndi Yohane, kuti apite ku phiri lalitali kwambiri ili. Ine ndikuzikonda zimenezo!

⁹⁶ Ndipo, mfundo ina, ngati mungandikhululukire ine chifukwa chotenga nthawi yochuluka, koma ine ndikukhumba kuti ndiyike pamaso pa omvetsera awa mmawa uno, kuti izi zinali ndi tanthauzo lina kwa izo. Atachoka pa phiripo ndipo akubwera kumatsikira pansi, funso linafunsidwa, “Kodi anthu amati Ine Mwana wa munthu ndine ndani? Ndani? Kodi anthu amati chiyani za Ine? Monga Ine ndiri ndi inu, ndipo ndawonetseredwa kwa inu, tsopano kodi anthu amati chiyani za Ine Mwana wa munthu?”

⁹⁷ Penyani zimenezo. Ndi chithunzi chokongola bwanji cha lero! Mutamulandira Khristu, mutadzazidwa ndi Mzimu, kodi anthu amanena chiyani za inu ndiye? Kodi anthu amati chiyani, kuti pamene iwo awona zochita zanu mutakondowezeka mpaka simungathe kukhala chete, misonzi yachisangalalo idzatsika m’masaya mwanu, pamene simungathe kutsitsa manja anu pamene iwo akuyimba nyimbo za Ziyoni; pamene simungathe kukhala chete, pamene muwona tchimo ndipo mukuyenera kuyankhula mwamtendere ndi mwakachetechete ndi iwo? Kodi anthu amati chiyani za izo? Kodi anthu amanena chiyani, kuti pamene iwe ukugona, kufa, womvetsa chisoni, watsoka, mu chikhalidwe chakufa, ndipo inu nkumupempha mwana wina wa Mulungu kuti agwirizane nanu mu pemphero la machiritso anu; ndipo inu nkuvomereza zolakwa zanu, ndi kuchiyika chinthucho pamaso pa Atate, nkuti, “Atate, ndikhululukireni ine, ndipo tsopano ndikulandira Khristu ngati mchiritsi wanga,” ndipo mwakhala bwino?

“Kodi anthu amati Ine Mwana wa munthu ndine ndani?”

⁹⁸ Ine ndikuyang’ana pa omvetsera, ndipo ena a inu ine ndikuwadziwa; momvetsa chisoni, zaka zapitazo, akufa ndi khansa, siteji yotsiriza. Ena a inu mmitundu yonse ya mawonekedwe, kapangidwe, akhungu. Ndipo Mulungu, mwa chisomo Chake, anakuchizani inu. Ndipo pamene inu mukupereka umboni wanu wamphamvu pamaso pa anthu . . .

“Kodi anthu amati Ine Mwana wa munthu . . .?”

⁹⁹ Kodi iwo ananena chiyani za izo? Mmene chithunzicho chasinthidwira kuyambira tsiku limenero, ngakhale chinali chakuda momwe chinaliri! Ena amati, “Ndi kutengeka.” Ena anamutcha Iye, “Bezebule.” Ena amati, “Ndi kuwerenga maganizo.” Ena amati, “Ndi kutengeka.” Ena amati, “Ndi kujijirika.” Ena amati, “Ndi zogirigisha.”

¹⁰⁰ “Koma inu mukuti chiyani za izo? Inu mukuti chiyani za chinthu ichi?”

¹⁰¹ Petro wopupuluma kawirikawiri amayankhula mopanda ulamuliro, koma nthawi ino sanatero. Iye anati, “Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo. Ine sindikusamala zomwe ena onsewo akunena. Izo ndi zimene ine ndikuzidziwa. Inu ndi Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo.”

¹⁰² Mvetserani. Tikhoza kutaya nthawi yambiri pamenepo. Koma tiyeni tipitirire. Yesu anati, “Wodala . . .” Ngakhale anthu angatemberere, ngakhale anthu angaseke. Anthu akhoza kunena kuti ndinu woyera wodzigudubuza. Anthu akhoza kukutchulani inu dzina lirilonse pansu pa dzuwa. Koma Iye anati, “Wodala ndi iwe, Simoni Mwana wa yonasi. Bambo ako. . .”

¹⁰³ Ndi izi apa tsopano. Mwakonzeka? “Pakuti thupi ndi mwazi sizinaulule izi kwa iwe. Iwe sunaphunzire izi kupyolera mu seminare ina ya chiphunzitso. Komanso iwe sunaphunzire izi kuchokera ku kulengeza kwina kwa zaumulungu za munthu wina. Thupi ndi mwazi sizinaulule izi kwa iwe, koma Atate Anga amene ali Kumwamba awulula izi kwa iwe.” Mukuona kumene izo zikuchokera? Kupyolera kwa Mphunzitsi, Mzimu Woyera, waziulula izo mwa vumbulutso.

¹⁰⁴ “Ndipo ine ndinena kwa iwe, iwe ndi Petro, thanthwe laling’ono. Ine ndi Thanthwe lalikulu. Ine ndine Mwalawapangodya, koma iwe ndi thanthwe laling’ono limene laikidwa pa Ine. Omanga anakusankha iwe. Sunadzisankhe wekha. Omanga anakusankha iwe. Angelo a Mulungu, usiku wina, akugwira ntchito mu miyala, anakuitana iwe, ndipo iwe unadzipereka wekha kwa Ine. Ndipo Ine ndinakudula iwe mmakonzedwe Anga anga. Ine ndinakupanga iwe momwe ine ndinkafuna kuti ukhale. Ine ndinachita kudulako; iwe unangoyima njii. Ndipo ine ndakuyika iwe tsopano ngati mwala waung’ono, kuti ulowererane ndi mwala wina, kuti utsogolere mwala umenewo; ndipo mwala *wu* ukutsogolera mwala *umenewo*, mwala *umenewo*. Ndipo simenti ya chikondi ikukubweretsani inu pamodzi, kupanga Maziko, chimene Ine ndiri, kuyikidwa pamodzi ndi mwala uliwonse umene umatchula Dzina Langa ndi kulandira vumbulutso ili.”

¹⁰⁵ “Ndipo pa thanthwe ili, vumbulutso la Mulungu, limene lidzayime nji ndi kudulidwa, (mwala, mwa vumbulutso), Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata zonse za gehena sizidzaulaka Iwo.” Kusonyeza kuti, ndithudi, zipata zonse za gehena zidzatsutsa izo, koma sizidzapambana konse.

¹⁰⁶ Ndipo mulole nditenge mphindi ino kuti ndinene ichi, mzanga, kuti, Mpingo wonse wa Mulungu wamoyo wamangidwa moona pa vumbulutso lauzimu la Ambuye Yesu Khristu. Ziribe kanthu kuti ndinu wophunzira bwanji, momwe mungakhalire wanzeru, momwe mungaganizire kuti mumadziwa Baibulo bwino, Satana amalidziwa Ilo bwino kwambiri kuposa momwe inu mumachitira. Koma kokha kupyolera vumbulutso, Mulungu kupyolera mwa Mzimu Woyera, Mphunzitsi wanu, anaulula kwa inu, kuti Iye amakupulumutsani ndi chisomo Chake.

¹⁰⁷ Ngati Iye angaulule kwa inu mmawa uno, mwa vumbulutso, kuti uku ndi kutha kwa zowawa zanu, uku ndi kutha kwa matenda anu, adierekezi onse kuchoka mu mazunzo

sadzagwedeza konse maziko amenewo, ngakhale dokotala aliyense atanena kuti izo nzolakwika. “Pakuti pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizingathe kuwulaka Iwo.”

¹⁰⁸ Ngakhale izo zitakhala zikutsutsa izo, komabe izo sizingakhoze kugonjetsa. “Pakuti pamene mdani adza ngati kusefukira, Mzimu wa Mulungu umakweza muyeso motsutsa izo,” nthawi iliyonse. Inu mukuziwona izo? Inu mukumvetsa izo? Tsopano, Yesu, akuwululidwa kwa ophunzira.

¹⁰⁹ Taonani mmunda wa Edeni, pamene Kaini anabweretsa nsembe mwa kupembedza, mofanana momwe Abele anachitira. Iye ankapembedza. Iye ankapereka ku mpingo. Iye ankapereka nsembe. Iye anachita chochita chirichonse chachipembedzo, chowala, chabwinoko, choyenera kwambiri, kuposa chimene Abele anachita. Iye anamanga guwa labwinoko. Iye analikongoletsa ilo. Iye anayika zowala ku kupembedza kwake. Inu mukuona kupsyinjika uko kukugwirabe ntchito pakati pa ana a Adamu? Iye anayika kukongola kwa izo, ndi zipatso za mmunda, ndi kakombo wamkulu. Ndipo iye, osati zokhazo, koma iye ankapembedza. “Pali njira imene imawoneka yolondola kwa munthu.” Koma, chimene iye anachita, iye ankapembedza kudzera mu chidziwitso. Iye sankapembedza mwa vumbulutso.

¹¹⁰ Ndipo ndi zotheka. Mumvetse izo tsopano. Mvetserani. Iwe utha kumapembedza kudzera mu chidziwitso. Ukhoza kumapita ku tchalitchi, mwa chidziwitso kuti iwe ukuyenera kuchita zimenezo. Koma kupita ku tchalitchi, mwanjira imeneyo, ndi kupembedza pachabe. Koma pamene pali chinachake chikuchitika pansu mu mtima mwako, izo zimakupanga iwe kumukonda Mulungu, mwanjira imeneyo iwe sungajombe ku tchalitchi, limenero ndiro vumbulutso, Mulungu akuwulula.

¹¹¹ Iwo analibe Baibulo nthawi imeneyo. Iwo analibe ngakhale pepala kapena sileti yoti agwirire ntchito. Iwo analibe masukulu a maphunziro. Chotero, Abele, mwa vumbulutso, chinawululidwa kwa iye ndi Mulungu, kuti, “Sikunali kukongola, kapena zipatso za mmunda, kapena ma apulo, zimene zinawathamangitsa iwo kuchoka mmunda wa Edeni, koma anali magazi.” Ndipo zinawululidwa kwa iye, ndipo iye anapita ndipo anakatenga mwanawankhosa. Mwa vumbulutso, iye anawoneratu Kudza kwa Mwanawankhosa Wolungama. Ndipo zinawululidwa kwa iye, chotero iye anakatenga mwanawankhosa. Ndipo mwa vumbulutso, anayipereka iyo kwa Mulungu, ndipo analandiridwa. Mpingo wonse unamangidwa pa vumbulutso lauzimu. Ndi zokongola bwanji!

¹¹² Tsopano, kufika kotseka. Iwo anali pa phiri. Ndipo Yesu atatha kukhala Mwana womvera; thupi, Mwanawankhosa, anali atatsogozedwa ndi Mzimu Woyera, Mulungu akuyenda mwa Iye.

“Ine sindinabwere kudzachita chifuniro Changa, koma chifuniro cha Iye amene anandituma Ine. Ndipo Iye amene anandituma Ine, Atate amene anandituma Ine, ali ndi Ine. Ndipo monga Atate andituma Ine, ndipo anapita ndi Ine, chotero Ine ndikutumani inu.” Sikuti Iye anangomutuma, koma Iye amapita naye Iye.

¹¹³ Ndipo Mulungu samangomuphunzitsa munthu ndi kumutumiza iye kunja ndi kulengeza kwa chomuchitikira china chaku seminare. Koma, ngati iye ali ndi zida, Mulungu amapita naye iye. “Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka kumapeto a m’badwo.”

¹¹⁴ Zindikirani, mokongola, oh, momwe Mawu amayendera limodzi! Momwe Mzimu Woyera umalimbikitsira Iwo mu mtima wa anthu, mwa vumbulutso ndi chikondi cha Ambuye Yesu. Penyani mwacheru.

¹¹⁵ Kumeneko, pambuyo pa kumvera, “pakamwa pa mboni ziwiri kapena zitatu,” mboni zabwino kwambiri zomwe zinaima pa dziko lapansi. Chikondi...Petro, Yakobo, ndi Yohane; chiyembekezo, chikhulupiriro, chikondi. Pansi pa mboni za chiyembekezo, pansi pa mboni za chikhulupiriro, pansi pa mboni ya chikondi; Mulungu anamuyika Mwana Wake, pamalo, pagulu, mwa kuwonetsera konse kutatu kwakukulu kwambiri (chiyembekezo, chikhulupiriro ndi chikondi) komwe dziko lidzadziwa.

¹¹⁶ Ndipo, apo, monga atate mmasiku akale ankamutengera mwana wake wamwamuna panja ndi kumuveka iye mwinjiro, ndipo amakhala ndi mwambo, ndipo pambuyo pake dzina la mwanayo limakhala chimodzimodzi monga la atatewo. Mwanayo amakhala wolowa wa zinthu zonse.

¹¹⁷ Ndipo Mulungu anamutengera Khristu pa phiri la chiwalitsiro, mu umboni wa chiyembekezo, chikhulupiriro, ndi chikondi, ndipo anamuphimba Iye ndi Mtambo. Ndipo Baibulo linati, “Zovala zake zinawala ngati dzuwa. Ndipo Liwu lochokera Kumwamba, akuti, ‘Uyu ndi Mwana Wanga wokonedwa.’”

¹¹⁸ Tsopano, Petro anasangalala yense, monga mwa nthawizonse. Iye anali munthu wachangu kwambiri. Ndipo ndikanakonda tonse tikanakhala achangu; nthawi zambiri iwe ukhoza kuyankhula zinthu zabwino mu ntchito zako zachangu. Koma Petro anangotengeka yense pamene anawona kwenikweni zimene zinachitika. Mulungu anali woti amulola iye kukhala ndi umboni mu kanthawi pang’ono chabe, iwo atapita kumusi. Koma pamene iye anawona, atayima...Panali zitatu apa: chiyembekezo, chikhulupiriro, ndi chikondi. Ndipo panali atatu atayima patsidya uko pa phiri: Petro, Yakobo, ndi Yohane, *apa*. Mose, Eliya, ndi Khristu, atayima *pamene*, mu kutsimikizira kwa atatu awa apa. Tsopano, iwo anayang’ana. Apo panayima Mose, poyamba; kenako panaima Eliya, mneneri.

119 Ndipo anthu ena amatifunsa ife, “Kodi ife tidzakadziwana wina ndi mzake tikadzakafika kumeneko?” Pamene, Eliya ndi Mose anali atapita, mahandirede ambiri a zaka. Osati kuti tidzangodziwana wina ndi mzake, ife tidzawadziwa iwo amene sitinawawonepo. Petro, Yakobo ndi Yohane, anali asanamuwone Mose, ndipo komabe anawazindikira iwo mu kuthwanima kwa diso, pamene iwo anali atayima pansu pa Mthunzi wa Wamphamvuzonse. Kodi chidzakhala chiyani pamene ife tidzayime Pamene? Ine ndidzamudziwa Sankey ndikadzamuwona iye. Ine ndidzadziwa liwu lake, ngakhale sindinamumvepo iye. Ine ndidzamudziwa Wesley. Ine ndidzamudziwa Moody, Calvin, Knox. Ife tidzawadziwa onsewo tikadzakafika kumeneko. Ife tidzatenga mbali yosiyana yoposa imene ife tiri pano. Tidzakhala mu kanthawi . . . kapena—kapena, mu chikhalidwe cha ulemelero. Petro, Yakobo, ndi Yohane anali. Chotero, mu chiwalitsiro chimenecho, ngati iwo akanawazindikira amuna, opanda chilema chimodzi, amene anali asanawawonepo kapena kuwona chithunzi chawo, amene anali atapita kwa mazana a zaka; koma, mu chifaniziro, anakhoza, mu kamphindi kanthawi kuwazindikira iwo, mosakaikira; zidzakhala bwanji pamene ife tidzakhale a ulemelero, titadzaima mu Kukhalapo Kwake? Kodi tidzadziwana wina ndi mzake? Ndithudi. Ife tidzamudziwa aliyense. Kupandamalire pang’ono kudzakhazikika pa ife, monga Mulungu ali wopandamalire.

Zindikirani. Ndikuyenera kutseka. Pamene iwo anayang’ana, ndipo Petro . . .

120 Monga momwe wophunzira wabwino weniweni wa seminare angati, “Inu mukudziwa, ine ndikukhulupirira mipingo yonse ndi yolondola. Ngati ndinu wa orthodox mu chikhulupiriro chanucho, ziribe kanthu, kotero ife tingokhala nawo Achimuhamedi ndi Achibudha, ndipo ife tikhala nawo onsewo pamodzi.”

121 Petro anati, “Ndi zabwino kuti ife tikhale pano, ndipo tiyeni ife tsopano timange akachisi atatu. Ife timanga seminare kuno ya Mose. Ife timanga seminare ya Eliya. Ndipo onse amene akufuna kupembedza pansu pa lamulo, ndi zina zotero, asiyeni iwo azipembedza.” Ndipo tsopano ife tikuzindikira. Iwo anayang’ana, ndipo Petro ndi iwo, akumuyang’ana Mose. Mose ankaimira lamulo.

122 Mulungu anawapatsa ana a Israeli lamulo chifukwa iwo ankafuna lamulo. Mulungu sankafuna kuti iwo akhale nalo ilo. Kumeneko ndi kusankha kwa munthu. Mu Eksodo 19, iwo anati, “Inu mutipatse ife chinachake choti tizichita, kuti chiyenerenze chipulumutso chathu. Ife tizisunga lamulo, ngati Inu mupereke ilo kwa ife,” mwakulankhula kwina. Koma, ilo silinali dongosolo la Mulungu.

¹²³ Ndi zabwino kungosiya kukonzekera, nokha, ndi kungogwiritsa ntchito dongosolo Lake. Ine ndimapeza izo kukhala zophweka kwambiri, kutenga dongosolo Lake.

¹²⁴ Apo panaima Mose, lamulo. Petro anati, “Chabwino, ena a ife timasunga lamulo.” Tsopano, palibe thupi lolungamitsidwa ndi lamulo.

¹²⁵ Chotero, chotsatira, lamulo la Mulungu litayima pamenepo; wotsatira, anaima, anali Eliya. Umo ndi momwe iwo anabwerera, mwadongosolo lachiwerengero. Wotsatira, anayima, anali Eliya, amene anabwera pambuyo pa Mose. Ndipo Eliya ankaimira chirungamo cha Mulungu, aneneri. Ndipo Eliya ankaimira chirungamo Chake, motero kuti Eliya anakoka moto kuchokera kumwamba ndipo unapha fifite. Ndipo iye ankaimira chirungamo cha Mulungu.

Chotero, Petro ankafuna lamulo la Mulungu ndi chirungamo cha Mulungu.

¹²⁶ Palibe munthu angapulumsidwe ndi lamulo. Ndipo ngati inu mulephera, kulakwitsa lamulo, pali chinthu chimodzi chokha chotsalira, ndipo ndicho imfa. Ndicho chirungamo cha Mulungu. Mulungu—Mulungu amafuna zimenezo. Lamulo lake lachiyero likuyenera kukhala . . . kukhala ndi chirungamo.

¹²⁷ Chotero, ndiye, Petro akuyankhula, akufuna kuti amange kachisi wake, ndipo anamufunsa Mulungu ngati iye angathe kuchita izo, kenako iwo anayang’ana mmbuyo ndipo anawona Yesu yekha.

¹²⁸ Lamulo linali litalephera. Tiyeni ife, mmawa uno, tichotse maso athu poyang’ana ku kudzilungamitsa tokha, kapena chinachake chimene ife tachita. Ine sindipempha lamulo. Sindingaweruzidwe ndi lamulo, chifukwa ndine wopanda lamulo. Palibe munthu amene ankasunga lamulo. Iwo samatha kusunga lamulo.

¹²⁹ Ndipo inunso simungadzipulumutse nokha. Inunso simungadzichiritse nokha. Ndipo ngati lamulo, mwa chifuniro chanu chopangidwa ndi munthu, inu munkafuna kuwonetsera izo ku dongosolo, ndiye pali chinthu chimodzi chokha chimasowekera ndi lamulo, ngati inu mulephera, ndicho chirungamo. Ndipo, chirungamo, ndiko kuweruzidwa ndipo nkufa kwa nthawizonse. Ichochimafuna kutheratu psyiti. Chifukwa, iye amene aphwanya mfundo imodzi ya lamulo ndi wolakwira lamulo lonselo. Chotero, inu mukuyenera kufa, koma Mulungu . . . pamene ife tiyang’ana pa lamulo la Mulungu, ndi kuyang’ana pa chirungamo cha Mulungu.

¹³⁰ Tiyeni tiponyere maso athu mbali inayo. Tiyang’ane *apa*. Apo panaima Yesu, akuimira chikondi cha Mulungu. Osati lamulo, osati chirungamo, koma mwa Iye munakumana kukwaniritsidwa kwa ziwiri zonse lamulo ndi chirungamo. “Uyu ndi Mwana Wanga wokonedwa.” Panalibenso zinthu

zodzipangira wekha. Muzimvetsera kwa mphunzitsi wanuyo. Ndi chifukwa chake Petro ankakhoza kunena kuti, “Inu ndi Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo.” Lamulo ndi chirungamo zinakwaniritsidwa mwa Khristu, ndipo ndi chikondi cha Mulungu kwa mtundu wa anthu. Chikondi cha Mulungu! “Mulungu analikonda kwambiri dziko lapansi!”

¹³¹ Mulungu wachifundo, mmawa uno, pamene ine ndikuchonderera omvetsera awa, sitikuchonderera lamulo, sitikupempha lamulo lililonse. Ife sitikufuna kuweruzidwa ndi kuyenera kwawo. Ine sindikufuna chirungamo Chanu, Ambuye. Ayi, osati kuti chiweruzo Chanu chibwere pa ine; ayi, Ambuye. Koma, ine ndikuchonderera chifundo Chanu.

¹³² Iye anati, “Mvereni inu Iye.” Chifukwa chiyani ndikuyenera kumumvera Iye? Iye ndi mmodzi yekha amene ali ndi chipulumutso. Maria, Yosefe, ndi oyeri ena onsewo anali anthu opambana, koma Iye yekha. “Mvereni inu Iye.” Iye ndi wopembedzera yekhayo. Iye ndi mkhalapakati yekhayo pakati pa Mulungu ndi munthu, ndiye Khristu Yesu.

¹³³ Nchifukwa chiyani ine ndizimumvera Iye? Lamulo silikanandipatsa ine mtendere; Iye akhoza. Chirungamo sichikanandibweretsera ine kalikonse, kutsutsidwa kokha. Iye amandipatsa ine mtendere ndi chiyanjantso. Lamulo limakhoza kunditsutsa ine, chifukwa, ngati ndidwala, lamulo limafuna kuti ndikhale ndi ziwiri zonse, malamulo a chirengedwe ndi chirungamo cha Mulungu, zimaperekedwa pa ine, chotero ine ndiyenera kulipira chilango. Koma ndikutembenezira zokonda zanga ndi maso anga, mmawa uno, kuchoka ku ziwiri zonse lamulo ndi chirungamo, ndi kuyang’ana pa chikondi cha Mulungu amene anandiyanjantisa ine kubwerera kwa Iye, kupyolera mu chisomo, ndipo osati kupyolera mu lamulo ndi kupyolera mu chirungamo. Koma, kupyolera mu chiyanjantso, Iye analipira mtengo kuti adzamubweretse munthu ndi Mulungu pamodzi, kuti adzawapange iwo amodzi.

¹³⁴ Uko mu Switzerland, osati kale kwambiri... Pamene ndikutsekera pa ndemanga iyi. Ambiri a inu ana ku sukulu, ine ndikuganiza inu mukadali nayo iyo, nkhani yakale imene sikuyenera kufa konse. Ngakhale, ikuzilala lero, mu dziko lathu, koma sizazilala ku Switzerland kumene iyo inachitikirako. Inu mukukumbukira ku sukulu yanu, mwa owerenga anu, za Arnold von Winkelried, ngwazi yaikulu ya Switzerland? Inu mukhoza kutchula dzina lake, lero, uko ku Swiss Alps, ndipo nkhope zawo zidzasintha mtundu ndipo misozi idzatsika m’masaya mwawo. Zaka zambiri zapitazo. . .

¹³⁵ Achi Swiss ndi anthu okonda mtendere. Iwowo ndi achi German amene, kalekale mu zaka zoyambirira, anapita kumusi kumapiri kumene kulibe miyala kapena kanthu. Koma iwo anagula. . . Iwo ali ndi luntha la achi German. Achi German

amaganiza kuti iye ndi mtundu wapamwamba, izo ndi zoon, koma iye akuyesera kupanga mfuti kapena bomba lomwe lidzagonjetse dziko lonse lapansi ndi luntha lake. Koma achi Swiss ndi munthu wokonda mtendere. Iye amapita kumusi ndi kumupangira iye a... amamupezera iye zipangizo zina, ndi kumupanga woyandikana naye kukhala woyang'anira, ndi kukhala mwamtendere.

¹³⁶ Kenako, kumtunda mmapiri aatali a Swiss, zaka zambiri zapitazo, pamene iwo anakhazikitsa wawo—ufumu wawo, kapena ndinganene kuti boma lawo, iwo sanali fuko lankhondo. Iwo anali fuko lokonda mtendere.

¹³⁷ Ndipo tsiku lina, pamene owukira anabwera ku dziko lawo ndipo anakawononga chirichonse chimene iwo anali nacho; kalikonse, kalikonse, ziribe kanthu chimene iwo anamanga. Iwo amagudubuzira miyala pansu mmapiri, ndipo izo iwo analibe nazo ntchito. Ndipo iwo anali ndi ankhondo achi Swiss ali kumbuyo mmunda pansu pa phirilo.

¹³⁸ Ndipo ndi zokongola kwambiri mu Switzerland, momwe ine ndinawawonera iwo, momwe iwo amalimira; ndi mmalo a m'zigwa; ndipo chotsatira ndi ng'ombe, ndipo kenako kutali kukwera paphiri ndi nkhosa, ndipo njira yonse pamwamba ndi pamene iwo amaweta mbuzi zawo.

¹³⁹ Ndipo momwe iwo aliri ndi kuyimba kumene awa aku America Hollywood otchedwa oyimba amazinyoza, sizimafanana ndi izo. Momwe iwo anakawombera lipenga lawo pamene avutitsidwa, kuti, ndipo woyandikana nawo aliyense ankathamangira pamodzi kuti akathandizire pamene pakhala chosowa china. Ndipo tsopano ife timagwiritsa ntchito izo ngati gulu loyimba za jazi, gwedemula. Oh, izo nzotero... Kuyipa kwake!

¹⁴⁰ Mvetserani, abwenzi. Ine ndipereka ndemanga ya bwana wanga: “Ngati Mulungu satumiza chiweruzo posachedwa kwa kam'badwo kachigololo aka ka anthu, Iye adzayenera adzadzutse Sodomu ndi Gomora, ndi kuwapepesa chifukwa chowawotcha iwo.” Uko nkulondola. Ndithudi. Iye ndi wolungama, ndipo sipangakhale china chirichonse chimene chingachitidwe koma Mulungu akuyenera kuchichita icho. Ndipo pamene chifundo chigwira manja Ake otsegula, thawirani kwa Iwo.

¹⁴¹ Ndipo uko, pamwamba pa phiri, kumene gulu lankhondo laling'ono ili linali ndi zida zomwe iwo akanakhoza kuzipeza, za zishango, ndi ndodo, ndi machekeka, ndi zina zomwe iwo anali nazo, ndi mafoloko. Mothandizidwa, gulu lankhondo lalikulu lachilendo linabwera monga ngati khoma lolimba la njerwa. Iwo anali munthu aliyense wophunzitsidwa, ndi mikondo yaikulu, ndipo iwo ankaguba chamtsogolo, pafupi, kuthandizira gulu la nkondo laling'ono lachi Swiss ili ku

phirilo. Iwo analibe chiyembekezo. Zonse zomwe iwo ankayesera zinali zonse zakuda ndi zamdima, ndipo panalibe chimene chikanawapulumsa iwo.

¹⁴² Patapita kanthawi, kuchokera pakati pawo, panadzabwera kufuula kwa mmodzi, Arnold von Winkelried. Ndipo anatulukira, ndipo anati, “Abale, lero ine ndifera Switzerland ndi ufulu wake.” Iye anati, “Timakonda dziko lakwathu ndi zomwe makolo athu anamenyera nkondo, ndi zimene makolo athu ankafuna kuti ife tikhale nazo. Ndipo, lero, chuma chathu chachikulu chiri pachiwopsyezo. Ndipo lero ndikupereka moyo wanga kwaulere ku Switzerland.” Iye anati, “Kutaliko, kuseri kwa phiri, kuli nyumba yanga yokondedwa, ndi mkazi wanga wokondedwa wokoma, ndi ana anga aang’ono, akundiyembekezera kuti ndibwereranso. Koma,” anati, “Ine sindidzawawonanso iwo padziko lapansi pano.” Iye anati, “Lero, ine ndifera Switzerland.” Iye . . .

Iwo anati, “Kodi iwe uchita chiyani, Arnold von Winkelried?”

¹⁴³ Iye anati, “Nditsateni ine. Ine ndiphwanya magulu ankhondo. Ine ndiphwanya boma lawo. Ndipo kenako inu mudzatenga chirichonse chimene inu muli nacho, ndi kumenya mwabwino momwe inu mungathere. Monga munthu wankhondo, mumenye ndi zomwe muli nazo, mopambana mmene mungathere.”

¹⁴⁴ Ndipo iye anakwezera manja ake mmwamba, ndipo iye anayang’ana pozungulira kumene mikondo yolemera kwambiri imabwera, pamene iye ankayandikirako. Ndipo anakwezera manja ake mmwamba ndipo anafuula, “Pangani njira ya ufulu!” Ndipo iye anawathamangira iwo amene ankayandikira khoma la njerwa. “Pangani njira ya ufulu!” Iye anafuula. Ndipo iye anathamangira ku mikondo yokhuthala kwambiri, ndipo anaponyera manja ake pa mikondoyo, ndipo anaisonkhanitsira iyo pa chifuwa chake ndipo anafa. Ndipo amuna achi Swiss, pamene iwo ankamutsatira iye, ndi zomwe iwo anali nazo. Icho chinapereka chisangalalo choterocho, mpaka icho chinaswa likulu lawo. Munthu aliyense anali kunja kwa malowo; iwo sanadziwe choti achite. Ndipo achi Swiss anathamangira ndipo anapambana chigonjetso, ndipo Switzerland sinakhalepo ndi nkondo chiyambireni. Izo zidzakumbukiridwa kwa nthawi yayitali ku Switzerland, bola ngati kuli Switzerland, Arnold von Winkelried adzakumbukiridwa.

¹⁴⁵ Koma, ameneyo ndi ngwazi yodabwitsa, inu mwaona, sizinayambe zafaniziridwapo konse, koma ndi chinthu chaching’ono, chinthu chaching’ono chabe, kwa tsiku lina pamene ana a Adamu . . .

¹⁴⁶ Pamene lamulo linalephera, ndipo pamene chirungamo cha aneneri chinalephera; kumene lamulo linali lofooka ndipo

silikanapulumsa, kupyolera mu nsembe ya mwanawankhosa. Magazi a nyama ndi mzimu wa nyama sizikanabwerera. Izo zinalephera. Satana ankadziwa bwinoko kuposa zimenezo. Ndipo pamene chirungamo cha Mulungu, komabe, kuyitanitsa moto ndi kuwotcha fifite, ndi ziweruzo zomwe aneneri amapereka ku dziko lapansi, anthu mopitirira ankapita ku chiwonongeko. Chiyembekezo chirichonse chinali chitapita. Mulungu anali atatumiza lamulo, Mulungu anali atatumiza aneneri; ndipo iwo onse anali atalephera. Ziyembekezo zonse zinali zitapita, kwa anthu.

¹⁴⁷ Tsiku lina, mkati mwa madera a Ulemelero, Mwana wa Mulungu anadzatulukira. Iye anati, “Lero, ndipita ndi kukamasula ana a Adamu.” Ndipo pamene Iye anayima kutsidyako, pamene ziyembekezo zonse . . .

¹⁴⁸ Mdierekezi amatha kuyika matenda pa ife, iye amatha kuyika tchimo pa ife, ndipo ife tinkayenera kuzitenga izo; chirungamo cha chilamulo chinkafuna izo. Ndipo ngati ife timalephera kulandira lamulo, limene ife tonse timatsutsidwa ndi lamulo, chirungamo chokha chitha kuchitika. Panalibe njira yotulukira; palibe chimene tikanachita.

¹⁴⁹ Koma Iye anatulukira patsogolo. Mngelo anati, “Inu muchita chiyani?” Iye anapita ku dziko lapansi.

¹⁵⁰ Ndipo Iye anati, “Tsopano inu, aliyense wa inu ana a Adamu, inu mutenge chimene ine ndakupatsani inu kuti mumenyere nacho, ndipo mumenye momwe inu mungathere, mopambana momwe inu mungathere.”

¹⁵¹ Ndipo Iye sanapeze konse malo ofooka, kudzera mu fioloje, kapenanso kumanga kwa maseminare, kapena kumanga matchalitchi; koma Iye anapita kumene kunali mikondo yochulukwa kwambiri, kumusi kupyola mu chigwa cha mthunzi wa imfa. Ndipo Iye anakasonkhanitsako imfa ndi matenda, ndi mikono Yake, kupita mu chifuwa Chake chomwe. Ndipo anatomizanso Mzimu Woyera pa Tsiku la Pentekoste, kukayika m’manja mwathu, ndi kufuna kuti mwana aliyense wa Adamu amenye mmene tingathere. Ngakhale mungasekedwe, ngakhale mungazunzidwe, ngakhale mungatchedwe “woyera wodzigudubuza,” china chirichonse; menyani momwe mungathere, pakuti chigonjetso ndi chotsimikizika. Ndipo mathokozo apite kwa Mulungu, mdani wazulidwa, maboma ake aphwanyidwa, ndipo Wolamulira wamkulu wa chipulumutso chatu akutsogolera, lero, mwa ubatizo wa Mzimu Woyera.

¹⁵² Oh, ana aamuna ndi aakazi a Adamu, nchifukwa chiyani mukukhala pano mpaka kufa? Tiyeni tidzuke ndipo tichite chinachake. Tiyeni titenge zomwe tiri nazo, ngati izo sizikuposa mlomo wachivundi womwe umatha kuyendabe. Tiyeni tipereke matamando kwa Mulungu. Tiyeni timuthokoze Iye chifukwa cha chipulumutso chatu.

153 Ngati iwe uli wochimwa, iwe sungathe kudzichotsa wekha kuchoka ku miyala ya dziko lino, imene Mulungu wakuchotsaniko inu ndi Uthenga. Koma, imani njii ndi kumulola Mulungu akuchekeni inu, kuti adzakuikeni inu pa Nyumbayo.

154 Ngati mukudwala, kumbukirani, Yesu anagonjetsa zonse imfa, gehena, matenda, manda, ndi zonse, pamene Iye anakuferani inu pa Kalvare. Tiyeni titenge zomwe tiri nazo mmawa uno, ndi kumenya nkhondo momwe tingathere.

155 Pamene ife tikuweramitsa mitu yathu mu mawu a pemphero; ndipo ngati ine ndingamufunse mlongo kuti abwere ndi kudzaimba limba, nyimbo ina yabwino. Pamene ife tonse . . .

156 Anthu anzeru, oganiza bwino, kodi inu mukuyamikira, mmawa uno, imfa ya Ambuye wathu Yesu? Mipingo yanu sigwira ntchito, ngakhale, yabwino momwe ingakhali. Masukulu anu adzalephera momvetsa chisoni, ngakhale, abwino momwe angakhali. Dokotala wanu adzalephera momvetsa chisoni, wabwino momwe angakhali. Koma, mmawa uno, tiyeni titembenuze mawonedwe athu, tiyeni titembenuze maso athu kuchoka ku malamulo a matchalitchi ndi zipembedzo, ndi ofesi ya dokotala, ndipo zabwino momwe izo zonsezo ziriri, ndipo tiyeni timvetsere Liwu lija likubwera kuchokera ku Mthunzi umene ukutiphimba ife mmawa uno, “Uyu ndi Mwana Wanga wokonedwa; mvereni inu Iye.”

157 Wokonedwa Atate Akumwamba, modzichepetsa monga Akhristu angayandikire, ife tikubwera mmalo mwa otayika ndi osowa. Atengeni mawu awa, lero, ndipo, oh, Mzimu Woyera umene ukutsogolera Mpingo, aphunzitsireni ana Anu kwa Mulungu, lero. Ambiri mwina anagwera mmbali mwa njira, ndipo sakuidziwa njira ya Mulungu panonso. Iwo akhala amdima ndipo achititsidwa mdima, ziyembekezo zawo zalephera, koma mulole iwo awonenso Kalvare kachiwiri, kumene Inu munagwira mivi yamoto ya mdani wa imfa, mdani wa matenda, mdani wachisoni, mdani wa anthu onse. Ndipo pamenepo Inu munaziyika izo mchifuwa Chanu, ndipo munathyola njirayo. Ndipo kudutsa kutsika mthunzi wakuda umenewo, mmawa uno, ife tikuwona Kwathu mu Ulemelero.

158 Monga von Winkelried ananena, “Kuseri kwa phirilo kuli nyumba, iwo akundidikirira ine kuti ndibwere, koma iwo sadzandiwonanso ine.”

159 Koma, Yesu, Inu simunati, “Iwo sadzandiwonanso Ine konse.” Inu munati, “Mu nyumba ya Atate Anga muli nyumba zambiri. Ine ndipita ndi kukakonza imodzi, ndipo ndidzabwera ndi kudzakutengani inu, ndi kudzakulandirani inu kwa Inemwini.” Momwe ife timalemekezera imfa yochirimika ya Winkelried; koma, iye anali wachivundi, iye anangokhoza kufa ndi kusiya mmbuyo. Koma Inu munabwera kudzafa

ndi kudzawombola, ndi kutibweretsa ife, osati kuchokera kwa okonedwa athu, koma kupita kwa okonedwa athu; osati kuchokera ku nyumba zathu, koma kupita Kwathu. Ndi kudzadula mzere kudutsa mu mdima wa imfa, kuti ife tidzathe kuwona kuseri kwa chophimba kumene kuli madalitso a Mulungu.

¹⁶⁰ Ndipo tsopano, lero, Atate Wokonedwa, ngati pali aliyense wa ana Anu amene Inu mwawaphulitsa ndi Uthenga, kuchokera ku miyala ya moyo, ndipo mukukhumba kuwapanga iwo chomwecho, ndipo mwakhala mukudula pa iwo mmawa uno, ndi kuwadula iwo, ndi kuchotsa zizolowezi zawo, ndi maganizo awo oyipa, ndi miseche yawo, ndi kubwerera mmbuyo kwawo. Ndipo tsopano Inu mukufuna kuti muwakhazikitse iwo kachiwiri, ndi kuwayika iwo mu Nyumbayi. Kodi Inu mungalankhule kwa mitima yawo pakali pano?

¹⁶¹ Ndipo pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa, kodi pangakhale mwana wina pano, lero, amene wasochera pa njirayi, kapena mwinamwake sanabwere pa njirayi? Koma inu mukumverera, lero, kuti mukufuna kuphatikizidwa; mukufuna kukhala mwala woyikidwa mu Nyumba ya Mulungu? Kodi mungakwezere dzanja lanu kwa Khristu, kunena, “Khristu, dulani chidziko changa.”

¹⁶² Mulungu akudalitseni inu kumbuyo uko, mnyamata wamng’ono. Mulungu akudalitse iwe, dona. Mulungu akudalitseni inu, bwana. Mulungu akudalitse iwe, mlongo wanga. Mulungu akudalitseni inu. Wina wakenso?

¹⁶³ Tsopano ndi mitu yanu yoweramitsidwa, pamene ife tikuyembekezera pa Mzimu Woyera, ndipo inu mukudziwa ngati inu mumamulephera Mulungu kapena ayi. Kodi inu munalephera kupita pamene Mgonjetsi wanu wamkulu anati, “Bwera, unditsate Ine. Nyamula mtanda wako, udzikane wekha, bwera unditsatire Ine. Ine ndidzaphwanya malikulu a mdani. Ine ndidzaphwanya malikulu a tchimo. Ine ndidzaphwanya malikulu a matenda. Ndipo inu munditsate Ine ndi kumenya mwabwino momwe mungathere, chifukwa ndidzapanga dzenje kudutsa izo, ndipo nyumba zathu zidasungidwira ku Moyo Wamuyaya.”

¹⁶⁴ Kodi ndinu mlendo wotalikana ndi Mulungu? Mungokweza manja anu, limodzi. . . Mulungu akudalitse iwe, mnyamata wamng’ono. Winanso amene sanakwezepo manja awo, koma kukweza mmwamba dzanja lawo. Kutu, “Ndikumbukireni ine, M’bale Branham, lero. Ine ndikufuna tsopano kuti ndibwere kwa Khristu. Ine . . .” Mulungu akudalitseni inu, mlongo.

¹⁶⁵ “Ine ndikufuna tsopano ndibwere kwa Khristu, kuti ndidzadulidwe ndi makina Ake. Chinachake mmawa uno chakhudza mtima wanga. Ine ndagwedezeka, pansu mkati mwa ine. Ine yense ndayikidwa kumbuyo kuno ndi zizolowezi

zachidziko, litsiro ndi matope padziko lapansi zavundukula . . . zandiphimba ine. Koma Uthenga, lero, wandivundukula ine, ndipo ine ndikuyima monga wolakwa pamaso pa Mulungu, ndipo ine ndikuzidziwa zimenezo. Ndipo ine ndikufuna Mulungu anditenge ine ngati mwala, lero, ndi kundidula ine, ndi kudzandipatsa ine chivomerezo cha Ambuye Yesu ndi Mzimu Woyera, ndi kundiyika ine mu Ufumu Wake. Ine ndikufuna ndivundukulidwe lero. Pamene ine ndavundukulidwa, ndikufuna kuti ndichekedwe ndi kuyikidwa mu Ufumu Wake.” Kodi inu mungakweze manja anu kwa Iye, ife tisanakhale ndi pemphero kwa a—wochimwa? Chabwino.

¹⁶⁶ Pali manja foro kapena faivi omwe akwezedwa mmwamba. Ine ndikupemphererani inu. Tsopano ife tiribe, mwinamwake, njira yopangira kuyitanira kuguwa, mwinamwake ngati inu muti mudikire mphindi zochepe chabe. Ine ndikupita . . . Ndikatha kupempherera odwala, ine ndikufunani inu kuno, inunso. Koma ine ndikupemphererani inu tsopano, kuti Mulungu angopereka chinachake chapadera kwa inu pa nthawi ino.

¹⁶⁷ Atate Athu a Kumwamba, zinalembedwa mu Mawu Anu Oyera, molingana ndi zolemba za mlembi Wanu, Mateyu Woyera, mutu wa 5, ndime ya 24, “Iye amene adzamva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye amene andituma Ine, ali nawo Moyo wosatha; sadzabwera ku chiweruzo, koma wadutsa kuchoka ku imfa kupita ku Moyo.”

¹⁶⁸ Imvani kupempha kodzichepetsa ndi kofooka kwa kapolo Wanu, kwa aliyense wa awa amene akweza manja awo. Inu munati, “Palibe munthu angabwere pokhapokha Atate Anga atamukoka iye.” Ndipo Inu mwakhala mukukoka, mmawa uno, ndipo iwo amva, ndipo iwo akweza manja awo. “Chikhulupiro chimadza pakumva, ndipo kumva Mawu.” Ndipo ine ndikukuthokozani Inu chifukwa cha iwo lero. Ndipo ine ndikupempha kuti Inu muyeretse wokhulupirira aliyense. Ndipo muwadzaze ndi Mzimu Woyera, iwo amene ali ndi mitima ya njala, amene akhuthula dziko, mmawa uno, ndipo akufuna kuti adulidwe ngati mwala wokwanira kuyikidwa mu Nyumba ya Mbuye. Ife tikupempha izi mu Dzina la Khristu. Amen.

¹⁶⁹ Kodi inu simukumverera mosiyana basi? Kodi Mzimu Woyera sukungotenga Mawu a Mulungu ngati burashi yokhulira, ndi kumangokhula kuchotsa zinthu za mdziko? Kenako inu mukumverera mwatsopano. Tiyeni tiyimbe nyimbo yakale yaulemelero iyi, kamodzinsu, kwa ulemelero wa Mulungu, tsopano. “Kuli Kasupe amene ali wodzazidwa ndi Mwazi, wochokera mmitsempha ya Emanuele.” Tonse palimodzi tsopano. Chabwino.

Kuli Kasupe wodzazidwa ndi Mwazi,
Wochokera mmitsempha ya Emanuele,

Ndipo ochimwa amadziponyera pansi mu
 kusefukirako,
 Amataya . . . madontho awo a zolakwa.
 Amataya madontho awo onse a zolakwa,
 Amataya madontho awo onse a zolakwa;
 Ndipo ochimwa amadziponyera pansi pa
 kusefukirako,
 Amataya madontho awo onse a zolakwa.

¹⁷⁰ Ine ndikufunsani inu chinachake pakali pano. Ndi angati akumverera kuti machimo anu onse ali pansi pa Mwazi? Kodi inu mungangokweza dzanja lanu. “Ine tsopano ndikukhulupirira kuti Mulungu wandikhulukira ine, ndipo ine—ine ndi mwana Wake.” Oh, mai!

Tsopano, wakuba pakufa, anasangalala
 kuwona
 Kasupe ameneyo mu tsiku lake.

Iye anali kufa. Iye anasangalala kuwona Kasupe mu tsiku lake.

Pamenepo ine, woyipa monga iye,
 Tsukani machimo anga onse.

¹⁷¹ Pamene ife tikuyimba ndime iyi, ndipo kenako tifika pa kolasi, ine ndikufuna kuti mugwirane chanza ndi winawake amene wakhala pafupi nanu. Munene, “Mulungu akudalitseni inu, m’bale Wachikristu, mlongo,” aliyense amene ali. Tsopano, tiyeni tiyimbe kwa Ambuye tsopano. Choyamba, tiyeni—tiyeni tikweze manja athu, ngati tingathe, ndi kuyimba, “Wakuba pakufa,” tsopano, pa kolasi, kenako tigwirane chanza.

Wakuba pakufa anakondwera kuwona,
 Atate, ife tikukupembedzani Inu tsopano.
 . . . Kasupe mu tsiku lake;
 Ndipo pamenepo ine, ngakhale woyipa monga
 iye,
 Tsukani machimo anga onse.
 Tsukani machimo anga onse,
 Tsukani machimo anga onse;

Tsopano gwiranani wina ndi mzake pa dzanja.

Ndipo pamenepo . . .
 Tsukani machimo anga onse.

¹⁷² Momwe ife tiriri okondwa lero, monga okhulupirira Achikristu, monga nzika zimzathu za Ufumu, kuti Mulungu watsuka machimo athu onse, ndipo watipanga ife zolengedwa zatsopano mwa Khristu Yesu! Tsopano, kodi ndinu okondwa chifukwa cha Ambuye? Zopambana!

¹⁷³ Tsopano kumbukirani, abwenzi, misonkhano ibwereranso kuno madzulo uno. Mulungu akudalitseni inu.

174 Ine ndinatenga nthawi yotalikirapo, mmawa uno, kuposa momwe ine ndimafunira kutero. Ine ndiri ndi chochita nthawi yomweyo, ukatha msonkhano. Ndipo ndine woti ndikumane ndi ena a inu abwenzi okonedwa. Ine ndikudabwa ngati zingakhale zotheka ngati ife tingayimitse izo mpaka madzulo uno, pamene ine ndibwererensho ku misonkhano usikuuno. Chifukwa, ine basi. . . ine ndimaganza kuti ndikhala nditatsiriza ikamakwana leveni, ndipo tsopano ife tiri ndi. . . Ndi angati ati apempheredwe? Tiyeni tione manja anu akukwera mmwamba, paliponse. Ife tiri ndi omvetsera ambiri oti tiwapempherere.

175 Ndipo ine ndinakuuzani inu momwe mwamuna wa Chilutera uja, kumtunda uko, anandilemba ine kalata yoteroyo ndipo ananditsutsa ine, ndipo anati, “Mwamuna amene analalikira kwa anthu,” zomwe ine ndinachita, “ndipo anganene kuti mdierekezi sangathe kuchiritsa,” ndi zina zotero. Ndipo ndinamuyankha iye modekha momwe ndikudziwira.

176 Iye analembanso, kalata, ndipo anati, “Ndikufuna kukumana nanu ku Msonkhano wa Amuna Azamalonda.”

177 Ndipo ine—ndipo ine ndinamufunsa M’bale Moore ngati iye angamupatse iye malo. Iye anati, “Inde.”

178 Ndipo iwo ananditengera ine uko ku seminare ya Chilutera, ndipo anakonza chakudya chamadzulo kumeneko, kumene ophunzira onse ndi aphunzitsi amenewo. Ndipo uyu anali mphunzitsi wamkulu; iye anakhala pafupi ndi ine. Ndipo tinadya chakudya limodzi. Ndipo iwo anali achi German. Ndipo iwo anali ndi—a—a chakudya chamadzulo chachikulu chitakonzedwa. Ndipo a—madona onse ankayembekezera pa ife, ndi zina zotero. Mgonero utatha, mphunzitsi wamkulu wa Lutheran uyu, wa koleji ya Lutheran, anaimirira ndipo anati, “M’bale Branham, ine ndakubweretsani inu kuno kwa cholinga chimodzi.” Iye anati, “Ndiko kuti, ife tikufuna kuti timupeze Mulungu mu ubatizo wa Mzimu Woyera.” Ine ndinamuyang’ana iye; ndinamuyang’ana M’bale Moore. Ndipo M’bale Moore anandiyang’ana ine. Iye anati, “Ine ndinakutsutsani inu, ndipo ndikupepesa.” Anati, “M’bale Branham, inu mukulondola, ndipo ine ndikukupemphani inu mundikhululukire ine. Ndipo tsopano ife tikufuna ubatizo wa Mzimu Woyera.” Anati, “Ife taona zomenya mipando zochuluka ndi kung’amba zinthu, koma,” anati, “ife tikufuna Mzimu Woyera weniweni.”

179 Ine ndinati, “Kodi inu mukukhulupirira?” Iye anati. . . Ine ndinati, “Kodi seminare ya Chilutera ndi chiyani. . . Kodi chipembedzo cha Chilutera ndi chiyani?”

180 Anati, “Ife sitikusamala chimene chipembedzo cha Chilutera. Ife tikufuna Khristu.”

181 Ndipo Bob Schuler ndi iwo, mkonzi wa Christian Herald, ndi iwo, anali atangolandira kumene Mzimu Woyera, bwenzi la

pamtima la Billy ndi onse amenewo. Abale amenewo ali ndi njala ya Mzimu Woyera. Ndipo kenako ine ndinati . . .

Iye anati, “Iwo ndi wa a Lutheran?”

Ine ndinati, “Iwo ndi wa, ‘Aliyense amene afuna, muloleni iye abwere.’”

Iye anati, “Kodi ife tingaulandire bwanji Iwo?”

Ine ndinati, “Kodi ndinu woona mtima kwenikweni?”

¹⁸² Iye anati, “Inde, M’bale Branham, kuchokera mu kuya kwa mtima wathu.”

Ine ndinati, “Nanga bwanji ophunzira inu?”

¹⁸³ Dzanja lililonse linakwera mmwamba, ndipo misozi ikuyenderera pansi pa masaya awo. “Ife tikufuna Yesu.”

¹⁸⁴ Ine ndinati, “Sunthirani mmbuyo mbale zanu. Tengani mabenchi anu, akankhireni iwo pakhoma.” Munthu aliyense anatero, njira yonse mozungulira. Ine ndinati, “Tsopano gwadani pansi ndipo mutembenezire nkhope yanu ku khoma, ndipo muyambe kumupempha Mulungu Mzimu Woyera.” Ndipo ine ndinamuuza M’bale Moore kuti ayime ndi kupemphera. Ine ndinapita, ndikuyika manja pa aliyense, ndipo ophunzira onse sevente-thuu, ndi mphunzitsi wamkulu, analandira ubatizo wa Mzimu Woyera. Ndipo iwo akugwedeza dziko limenero ku mtunda uko, ndi zozizwitsa ndi kugwira ntchito kwa Mulungu. Iwo akumakhala ndi misonkhano ya machiritso ndi chirichonse, seminare ya Lutheran.

¹⁸⁵ Oh, ine ndikhoza kuyimba mokhutira kwa mtima wanga! Chifukwa chiyani? Pamene uli ndi njala ndi ludzu!

¹⁸⁶ Mkazi wosauka uyu, wamng’ono wagona apa, akufa ndi khansa, ndithudi iye ali ndi njala ndi ludzu, mmawa uno, kuti Mulungu amuchiritse iye. Ndipo mulipo ambiri a inu mwakhala pamenepo ndi vuto la mtima. Ndithudi. Inu mufa nthawi yomweyo, ngati Mulungu sakuchizani inu. Pali ambiri amene ali ndi matenda ena, omwe ndi oyipa kwambiri. Koma, mzanga, usayang’ane ku chirungamo; sungathe kulipira chirungamo. Usayang’ane ku lamulo, chifukwa lamulo silingakhoze kusungidwa. Koma, uyang’ane kwa Yesu yekha, pakuti Iye ndi Amene anakuwombola iwe. Ndipo, kupyolera mu chikhulupiriro mu Dzina Lake, iwe ukhoza kuchiritsidwa mmawa uno.

¹⁸⁷ Ndipo ngati Mulungu angatumize achi Lutheran sevente—atumiki a Lutheran, kuti akalalikire Uthenga, ndi ubatizo wa . . . pa kusanjika manja. Yesu anati, pamene Iye anatipatsa ife nkondo zathu. . . Monga von Winkelried, iye anati, “Timenye ndi zomwe tiri nazo.” Izi ndi zomwe Iye ananena, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Mu Dzina Langa iwo adzatulutsa mizimu yoyipa, kapena ziwanda. Iwo adzayankhula ndi malirime atsopano. Ndipo ngati njoka idzawaluma iwo, iyo

siidzawavulaza iwo. Iwo adzayika manja pa odwala, ndipo iwo adzachira.”

¹⁸⁸ Ndipo tayang’anani pa kudula kwakukulu, kuzungulira dziko tsopano, Uthenga ukupitirira. Ndipo ana aamuna a Adamu, amene analandira chisomo cha Ambuye Yesu Khristu wathu, akumenyera njira yawo kuti adutse, ndipo kudula mzere pa mdani tsopano. Ndipo ife tikutenga momwe tingathere.

¹⁸⁹ Ndipo monga inu anthu abwino, mmawa uno, amene mumayamikira thanzi labwino, muzikumbukira izi pamene ife tikuzipempherera izo.

¹⁹⁰ Ndipo ine ndipempha kuti odwala afole ku mbali *iyi*, cha apa kumanja kwanga. Ndipo ngati akuluakulu angabwere ndi kudzawathandiza iwo, ngati mungafune. Ndipo ine ndikuwafunsa atumiki a Uthenga, ngati iwo angayime apa, pafupi, ndi kudzapemphera.

¹⁹¹ Ndiye musachoke ngati mungathe kupirira izo. Ife tikufuna kuti tipemphe kuyitanira paguwa kwina, mu mphindi yokha, mwamsanga momwe ife tingathere. Misonkhano siitha, ndi msonkhano wa machiritso uwu.

¹⁹² Tsopano folani mbali *iyi*. Ndipo ife timufunsa M’bale Neville, m’bale wathu wokonedwa, ngati iye ati achite mmene ife timapitirizira mwachizolowezi. Ngati iwo angathe. . . Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Ichu chinali chiyani? [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

Kungo khulupirira, kungo khulupirira,
Zinthu zonse ndi zotheka, kungo khulupirira;
Kungo khulupirira. . .

¹⁹³ Muyang’ane kuti? Kwa Yesu. Madokotala alephera. China chirichonse chalephera. Koma, “Uyu ndi Mwana Wanga wokonedwa, mvereni inu Iye.” Kodi Iye ananena chiyani? Iye anati, “Mvereni inu Iye.” Kodi Iye ananena chiyani? Kodi Iye ananena chiyani?

Kungo khulupirira,
Chifukwa chiyani? “Zinthu zonse ndi zotheka.”

Musawope, nkhoa zapang’ono, kuchokera
pamtanda kupita ku Mpando wachifumu,
Iye analowa. . .mu moyo, Iye anapita yekha
yekha; (. . .? . . .)
Iye. . .mphamvu pa dziko lapansi, mphamvu
zonse Kumwamba,
Zinaperekedwa kwa Iye chifukwa cha nkhoa
za chikondi Chake.

¹⁹⁴ Mphamvu zonse, za matenda, chirichonse, zaperekedwa kwa Iye.

Kungo. . .

Mvereni inu Iye. Kungo khulupirira!

. . . kungo khulupirira,
Zinthu zonse . . .

¹⁹⁵ Pamene lamulo lalephera, pamene adokotala alephera, pamene zinthu zonse zalephera, kodi Iye ananena chiyani? Kungo khulupirira. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

¹⁹⁶ Mahandirede ena, ine ndikuganiza. Ena a iwo akubwera mu zikuku. Mmodzi apa pa machira, pafupifupi kufa.

¹⁹⁷ Madokotala anu okondedwa, monga anthu odula thupi pakati, kapangidwe ka thupi, ndipo amayang'ana ndi kuwona chirichonse chimene iwo angathe, mu chidziwitso chawo, iwo amayesetsa kuti apulumutse moyo, koma nthawi zambiri iwo amalephera.

¹⁹⁸ Ndife okondwa kwambiri kuti Mtambo wowala uwu wa ulemelero umene unapachikika pa Iye, unati, “Koma uyu ndi Mwana Wanga wokondedwa.” Pamene lamulo linalephera, ndipo chirungamo chinalephera kuchitika, ndiye Mulungu anati, “Mvereni inu Iye.” Ndipo kodi Iye ananena chiyani? “Zinthu zonse ndi zotheke ngati mungangokhulupirira.”

Thandizani Inu kusakhulupirira kwathu.

¹⁹⁹ Ndipo monga atumiki a Uthenga, ife tikupita tsopano kuti tidzoze odwala, ndi kuyika manja pa iwo, pamene anthu opatulika a kachisi uyu akusonkhana pamodzi mu pemphero. Mulungu, dalitsani kuyesetsa kwathu, ndipo chiritsani odwala, tikupempha mu Dzina la Yesu.

²⁰⁰ Ndi mitu yathu yoweramitsidwa tsopano mu pemphero, ndipo pamene osonkhana akuyimba mofewa, *Kungo khulupirira*. M'bale Neville adzoza. Ine ndiyika manja pa odwala.

²⁰¹ Wokondedwa Atate Akumwamba, mwatsopano kuchokera kuseri kwa nsanja, pamene ine ndayima pakati pa imfa ndi moyo, pakati pa wochimwa ndi Chiweruzo, kuwalozera iwo njira yopulumukira, ine ndikuponyera izo kumbuyo kwawo tsopano ndi kuyika manja pa mkazi wodwala uyu. Ndipo pamene okondedwa ayima, akuyang'ana pa iye, palibe chinthu chimodzi chimene chingathandize tsopano koma Inu, ine ndikuyika manja pa iye, monga Inu munadzodzera . . .



KUKHAZIKITSIDWA KWAUZIMU CHA56-0923
(Spiritual Adoption)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lamlungu mmawa, Seputembara 23, 1956, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2023 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org